

M'BADWO WA MPINGO

WA TIYATIRA



Tsopano usikuuno ife tiri . . . Basi ife tisanapite mu m'badwo waukulu uwu wa mpingo . . . Ine—ine ndikungoyembekeza Ambuye wathu atsanulira Mzimu Wake pa ife basi . . . ndipo atidalitsa ife kachiwiri. Ndipo ife titha kungogunda zazikuluzikulu zokhazo tsopano chifukwa, pa chochitika chachikulu chimene chikubwera, ife tikhala pano sabata yonseyi. Ndipo, oh, usiku wathawu ife tinali ndi nthawi yaulemelo chotero!

² Chabwino, tsopano basi ife tisanawerenge Malemba, kodi ife tingangosintha athu—malo athu kwa mphindi pang'ono ndipo tiime ku mawu a pemphero.

³ Atate athu Achisomo Akumwamba, ife tikubwera mu Dzina lokwanira zonse la Ambuye Yesu, podziwa kuti tsiku lina Inu mudzabwera. Ndipo ife tikuyesetsa kuti tiikonzekeretse mitima ya anthu kuti ilandire vumbulutso lalikulu ili kuti Inu ndinu Mwana wa Mulungu wamoyo; osatiwakufa, koma wamoyo kwanthawizonse; ndipo mukukhala mu Mpingo Wanu ngati Mboni ya Pentekoste, ya nthawi yayikulu iyo pamene nthawi yotsitsimutsa idzabwera kuchokera mu Kukhalapo kwa Ambuye. Ndife okondwa kwambiri kusangalala nazo nthawi zimenezo kumusi kuno zitatha zaka naintini handiredi.

⁴ Ndipo, Atate, ife modzichepetsa tikuweramitsa mitu yathu polemekeza amuna opambana awa kudutsa mibadwo, nyenyezi zimenezo zimene Inu munazigwira mdzanja Lanu, zimene Inu munati zinali, “angelo a Mibadwo ya Mpingo,” atumiki. Momwe ife tikukuthokozerani Inu chifukwa cha Paulo Woyera wamkulu, waku Efeso. Momwe ife tikukuthokozerani Inu chifukwa cha Ireniasi, O Ambuye, Ireniasi wa wantchito Wanu wamkulu; ndi chifukwa cha Martin Woyera; ndipo usikuuno chifukwa cha Columba Woyera. Ambuye, momwe ife tikukuthokozerani Inu chifukwa cha amuna amenewa. Mkatikati mwa Chiroma chamdima, chikunja chikubwera mu mpingo, iwo anayima zolimba chifukwa cha Uthenga wa chipentekoste ndi mdalitso, kuyankhula mmalirime, ndi—ndi zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa, kuchiritsa odwala, ndi kuukitsa akufa.

⁵ Ambiri a iwo, Ambuye, anakhadzulidwa pakati, ndipo anaphedwa, ndi kudyetsedwa kwa mikango; zinthu zazikulu zinachitika. Dziko lapansi linasambitsidwa ndi magazi a olungama. Ndipo, Atate, magazi awo akufuula lero motsutsa mpingo woyipa, wachigololo uwo. Ndipo Inu munati, tsiku

lina pamene Inu munatsanulira . . . “Mngelo anatsanulira mbale yake pa ilo, ndipo ma—magazi a wofera aliyense anapezeka mmenemo.”

⁶ Ambuye, tithandizeni ife kuti tikhale . . . tikhale okonzeka kuima tsopano, chifukwa nthawi ikuyandikira. Pamene ife tikuwona chirombo chanyanga ziwiri ichi chikukwera kuchokera padziko lapansi, osati kuchokera mu khwimbi ndi unyinjira wa anthu, “Chokhala ndi nyanga ngati mwanawankhosa, koma chimalankhula ngati chinjoka.” Ife tikukhulupirira kuti ora limenelo layandikira tsopano, Atate, pamene mipingo iyi ikudzipangira yokha chitaganya pamodzi, “Kupanga fano kwa chirombo”; ndipo zidzakhala zoyipa pa gulu limenelo, Ambuye, limene silidzalowa. Kukanizidwa kumene kudzabwera, koma mu ora limenelo Inu munalonjeza kuti mudzawutenga Mpingo Wanu. Tithandizeni ife, Ambuye.

⁷ Dontho limodzi lamadzi lisanagwe, Nowa anali mu chombo. Moto usanakanthe Sodomu, Loti anali atachokapo. Atate, ife tikukhulupirira, mphamvu za atomiki zisanaliphulitse konse dziko lapansi kukhala zidutswa, Mpingo udzakhala utachokapo. Ndife okondwa kwambiri, Ambuye. Ndipo, ife tikudziwa kuti mabomba apachikidwa mlengalenga, usikuuno.

⁸ Ndipo ife tikhoza kuyang’ana cha Kumwamba ndikumuwona Mwana wa munthu akudzuka pa Mpandowachifumu Wake kuyamba kubwera cha ku dziko lapansi ku Mkwatulo wa Mpingo Wake, ndipo tikudziwa kuti mapazi Ake ofunikira sadzapondetsa pa dziko lapansi lochimwa ili panthawi imeneyo; pakuti monga Rabeka anakwera ngamira ndi kudzatsika pa ngamirapo, pakati kumene pa nyumba ya Abrahamu, uko mmunda iye anakakumana ndi mkwatibwi wake. O Mulungu, ndipo Mpingo udzakumana ndi Mkwatibwi wathu mu mlengalenga, “Pakuti ife omwe tiri ndi moyo ndipo tatsalira sitidzawalepheretsa kapena kuwatchinga iwo omwe akugona. Lipenga la Mulungu lidzawomba, akufa mwa Khristu adzawuka poyamba, ndipo ife tidzakwatulidwa nawo iwo palimodzi kukakumana ndi Ambuye (mmunda) mu mlengalenga, ndi kukhala ndi Iye kwanthawizonse.”

⁹ Oh, tithandizeni ife, usikuuno, Ambuye. Tipatseni ife kukoma kwa mizimu yathu, ndipo muchotse zowawa zonse ndi kusayanjanitsika zipite kutali kwa ife, ndipo mulole ife tikasungunuke *kwambiri* ndi Mzimu Woyera. Mulole Mngelo wa Mulungu alamulire usikuuno.

¹⁰ Ambuye, ine sindikudziwa choti ndinene kwa anthu awa. Tsopano, ine ndiri nazo mbirizakale ndi zinthu ndalemba za zomwe Inu munachita, koma izo zimatengera Inu kuti mumasulire zamtsogolo, chotero ine ndikupemphera kuti Inu mupereke izi kudzera mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

¹¹ Tsopano tiyeni ife titembenezire tsopano ku Bukhu la Chivumbulutso. Ndipo usikuuno ife tiri pa m'badwo wa mpingo wa...M'badwo wa mpingo wachinai, Tiyatira, m'badwo waukulu wa mpingo wodziwika kuti M'badwo wa Mdimu. M'badwo wa mpingo uwu ukuyamba mu 606 ndipo kenako ukudzathera mu 1520. Ine...Zinali zonse zimene ine ndikanakhoza kuchita, kuzitolamo. Ophunzira ambiri amamutenga—amamutenga Patrick Woyera kukhala nyenyezi kapena...aliyense...

¹² *Nyenyezi seveni* zinali “angelo seveni” a Mibadwo Isanu Ndi Iwiri ya Mpingo. Ife tikudziwa mawa usiku, mopanda kukaikira, Luther; ndipo kenako Wesley. Ife sitikudziwa kuti nyenyezi iyi ya mpingo wa ku Laodikaya idzakhala ndani. Ndizo...Ife tiri mu m'badwowo tsopano, wakhala ulipo kuyambira 1906 pakuyamba pa Pentekoste. Koma padzakhala mngelo amene ati adzauke yemwe adzasokoneze ziphunzitso zonse, adzawutenga Mpingo kuwukonzekeretsa kuti upite Kwawo. Tsopano, mbuye wina wa—wa...mu Mzimu, amene adzawuke ndi zizindikiro ndi zodabwitsa. Tsopano, ine ndikupemphera kuti Mulungu mutithandize ife kuti tidziwe izi.

¹³ Posankha izi, poyang'ana modutsa, Patrick Woyera anali munthu wopambana. Ndipo potenga zina za zolembedwa zaamakedzana, Patrick Woyera sanali Mkatolika. Iye anatsutsa mpingo wa Katolika. Ndipo mu nthawi ya Kukonzanso, chiphunzitso icho chimene iwo anali nacho chinakumbidwa, ndipo zinatsimikizira kuti Patrick Woyera ankatsutsa mpingo wa Katolika. Kut...Patrick Woyera anali ngati munthu wabungwe, iye anali ndi sukulu yake yake. Iye poyamba... pamene iye anadzagwidwa m'magombe a nyanja, iye, ndi azilongo ake aang'ono awiri omwe iye sanamvekonso za iwo. Iwo anatengedwa, mwinamwake kupita ku Roma ndi kukagulitsidwa ngati akapolo. Iye nayenso anadzatengedwa ndipo anakagulitsidwa ngati kapolo ndipo anapatsidwa ntchito yoweta nkhumba.

¹⁴ Iye ankaphunzitsa agalu kuti—kuti azisamalira nkhumba zake, ndi zina zotero; ndipo izo zimabwera ndi maliridwe osiyanasiyana ndi zinthu zomwe iye amawapatsa agalowo. Ndipo imeneyo potsiriza inali njira yopulumukirapo, pansu pa ngalawa, pamene agalu anadzamuphimba iye mpaka kuti iye analowa mnyanja. Kenako anadzabwera kumalo ake okongola, Ireland, ndipo anadzawapeza amayi ake ndi abambo akadali moyo apobe. Ndipo Patrick Woyera anali m—mphwake wa Martin Woyera wotchuka.

¹⁵ Amene, anali mmodzi wa opambana kwambiri omwe ife tinakhalapo nawo mu mzere wa aamuna kuchokera pa Yesu Khristu, anali Martin Woyera. Mpingo yake yonse inadzazidwa ndi Mzimu Woyera, iwo onse ankayankhula mmalirime, anali ndi zizindikiro ndi zodabwitsa, ndipo zozizwitsa, basi mitundu

yonse ya zozizwitsa zikuchitika. Iye anasunga chikhulupiriro cha Chipentekoste mkatikati mwa m'badwo wa mpingo uwo umene unkachita chikwati ndi Chikatolika, chikunja ndi Chinikolai zinakwatirana limodzi, kupanga bungwe, ndi kupanga A—Anikolai, omwe ife timawatcha iwo *nikao*, kutanthauza “kugonjetsa, kugonjetsa, kapena kuwalanda anthu wamba,” ndi kuwuchotsa Mzimu Woyera kuwupititsa kutali ndi osonkhana, ndipo “wansembe yekha ndiye ali woyera, munthu yekhayo.” Mukuona? Ndiyeno iwo nkumakhala mulimonse momwe iwo akufunira, ine ndikuganiza, ndipo bola ngati iwe walapa izo kwa wansembe. Ndiye iwo . . .

¹⁶ Tinapeza usiku wathawu, kuti—kuti iwo anawakhazikitsa iwo, kuti Konstantini anakhazikitsa bishopu woyamba, ndipo anaziika izo . . . anapereka nyumba izi kwa iwo, monga ife takupatsirani inu masiku ndi chirichonse zimene inu mwalemba. Ndiyeno iwo amakhala ndi phwando lalikulu la dzuwa kumeneke, limene limakhala tsiku la 21 Disembala, tsiku lalifupi kwambiri mu chaka. Ndipo anabweretsamo kenako mpatuko uwu, pokhala, kuti Iye anali “tsiku la dzuwa.” Mwaona, tsi—tsiku lobadwa dzuwa, iwo anabweretsa kubadwa kwa Yesu Khristu kuchoka Epulo mpaka Disembala 25.

¹⁷ Disembala 25. Kudutsa masiku asanu amenewo ndi pamene Aroma amakhala ndi zikondwerero zawo zazikulu, zisudzo, ndi zina zotero, ndipo ndi pamene iwo amakhala ndi phwando lalikulu lachikunja ili. Ndipo iwo amamuyika munthu uyu ngati mulungu iyemwini pamwamba apo, ndipo amamuveka iye ndi chirichonse. Ndipo iwo anali ndi mulungu wawo pafupi pomwe ndi iwo. Ndipo . . . ndi pamene anthu a zakazikwi-zamtzogolo anayamba kukhalapo, pomwe apo, chifukwa iwo ankaganiza kuti mpingo unali mu Zakachikwi pomwe apo. Mwaona, chifukwa iwo anali olemera, sankasowa kalikonse, boma ndi mpingo zonse pamodzi. “Zakachikwi ziri mkati,” chikadali chiphunzitso cha Chikatolika mpaka pano. Mukuona? Tsopano, “Zakachikwi zikuchitika,” chifukwa ife tikudziwa kuti zimenezo ndi zolakwika. Zakachikwi: Kudza Kwachiwiri kwa Khristu kukubweretsa Zakachikwi. Uko nkulondola.

Dziko lapansi likubuula, kulirira tsiku
lomasulidwa mokomalo,
Pamene Ambuye wathu adzabwereranso ku
dziko lapansi.

¹⁸ Tsopano, woyera wamkulu uyu apa anali Columba. Iye anali munthu wopambana wa Mulungu.

¹⁹ Tsopano, ine ndiri nayo mbiriyakale yake yomwe ndalemba apa. Choyamba, m'badwo wa mpingo wachinai, *Tiyatira*, iwo umatanthauza kukhala “wotairira, kumasuka,” kapena, “chimbuzi.” Mukuona? Iyo inangokhala nthawi yosayenerezeka kuyambira 606 mpaka 1500.

²⁰ Nyenyeziyo inali Columba, wochokera ku Ireland ndi Scotland, yemwe anali mphwake wa Martin Woyera; ndipo anakhala pafupifupi zaka sikisite pambuyo pa Patrick Woyera, ndipo chotero utumiki wake unayamba pafupifupi zaka sikisite pambuyo pa Patrick Woyera. Wake. . .

²¹ Iye sanalandire konse chiphunzitso cha Chiroma. Iye anali munthu wachikhulupiriro chachikulu. Iye anachikana chiphunzitso cha Chiroma; sanapite konse ku Roma, ndipo anachikana icho pamodzi. Ndipo, ine sindinathe kuwona kumene iwo anadzamukhazikitsa konse iye kukhala woyera. Monga iwo anachitira ndi Martin Woyera ndi iwo, iwo sanamukhazikitse iye kukhala woyera ndi Ireniasi chifukwa iwo anali akadali mu Mpingo umenewo umene unali ndi zizindikiro ndi zodabwitsa za Pentekoste, koma anakhulupirira. Iye sanatenge konse chiphunzitso cha Chiroma, pa ziphunzitso zawozo. Iye anatenga Baibulo ngati chiphunzitso kutengera amayi ake aumulungu, mlongo wake wa Martin Woyera, ndipo sanatenge konse ziphunzitso za Chiroma pa nthawi iliyonse. Iye ankaphunzitsa kuti zizindikiro za Marko 16 ziyenera kumutsatira wokhulupirira aliyense. Amen! Ine. . . Ndiwo mtundu wa munthu yemwe ine ndimamukonda; amakhulupirira. Inde, bwana.

²² Iye—iye anamva Liwu lomveka la Mulungu likuitana. Ndicho chizindikiro china chabwino kwa iye, mwaona. Ndiye palibe chomwe chikanamuletsa iye pambuyo pa zimenezo, iye anali atapita, uh-hum, uh-huh, iye anali panjira pamene iye anamva Mawu omveka a Mulungu.

²³ Chozizwitsa chimodzi. . . Ine ndiri nazo zingapo-. . . pansi pano, koma ngati ife tingangotenga ichi. Chozizwitsa chimodzi chinali chakuti pamene iye anapita ku mzinda winawake kumene Ambuye anamutumizako iye, ndipo mzindawo sunafune kuti umulandire iye, chotero iwo anapita kunja kumeneko ndipo anakayesera. . . anakawatenga oyimba, ndi zina zotero, ndipo anatekako zipatazo ndipo anayesetsa kuti asamvekenso iye poyimba, zing'wenyeng'wenye. Ndipo iye anayamba kulalikirira, ndipo izo zinawazimitsa a zing'wenyeng'wenyewo ndipo zipata zinatseguka, iye anapitirirabe, anakalalikirira mulimonse. Iye analitembenuza gulu lonse.

²⁴ Apa pali china chaching'ono chimene ine ndikufuna kuti ndingoyankhulapo. Iye anapita mu mzinda. Iwo anali ndi mizinda yawo ya khoma mmasiku amenewo, ndithudi. Chotero iye anapita ku mzindawo, ndipo iwo anamutulutsako iye. Iye anali akuchokako, ndipo mwana wamwamuna wa amfumu anadwala kwambiri, ndipo iwo anamutsatira pa msewu woyera wabwinoyo. Iye anabwererako ndipo anadzazigoneka yekha pa mwana wakufayo, ndipo iye anabwerera ku moyo.

²⁵ Mpingo wake unadzazidwa ndi Mzimu Woyera, iye sakanakhala ndi zina zocheperapo, pakuti membala aliyense wa mpingo wake ayenera kuti anadzazidwa ndi Mzimu Woyera. Ndipo iye anatsutsa ndipo anadana kwambiri ndi ufumu wolowezana wa Roma. Ine ndikukhulupirira iye anali nyenyezi ya m'badwo. Kodi iye amachita chiyani? Ndi kuyankhula mmalirime, ubatizo mu Dzina la Ambuye Yesu, kuchita zinthu zomwezo zimene iwo anaziya. Ngati Mulungu ali wopanda malire, ndipo ndi momwe Iye anakhazikitsira Mpingo Wake pachiyambi, izo ziyenera kukhalabe zofanana, ndipo ziyenera kutero (ngakhale mwa ochepe) njira yonse mpaka pansu; pafupifupi kufinyidwira panja *apa*, kubwereranso kudzera mwa Lutera.

²⁶ Tsopano, ife tikufuna kuti tiyambe tsopano, ndipo tiwone ngati ife tingayambe kutenga zina za ndime izi tsopano, pa . . . ife tiyambira pa ndime ya 18:

. . . *kwa mngelo wa mpingo wa Tiyatira lemba; . . .*

²⁷ Kodi inu munazindikira awa—malonje awa? Mauthenga awa akupita kwa mngelo, kapena mtumiki wonyamula Kuwala kwa m'badwo wa mpingo umenewo. Mukuona? Tsopano, usiku wathawu ife tinapeza, mu kutsekera kwa m'badwo wina uwu wa mpingo wa—wa Pergamo, kuti mngelo wa mpingo (pakugonjetsa mu m'badwo wa mpingo uwu) adzalandira mwala. Ndipo mu mwala uwu . . .

²⁸ Tsopano, ife tawutenga “mwala” umenewo ndipo tawuphiphiritsa, iwo ukutanthauza “thanthwe.” Ndi chiyani chimenecho? Mngeloyo akanadzakhala mmodzi wonga Petro, wotchedwa “mwala.”

²⁹ Mupeza kuti dzina lanu limakhala ndi chochita pa moyo wanu. Tsopano, ine sindingathe kupita mochulukira za zimenezo, chifukwa mdierekezi ali ndi mawerengedwe abodza; ife tikudziwa zimenezo; anthu amayamba *kumverera*, ndi zina zotero monga choncho, zomwe zimakalowa mu zamizimu. Ndipo zamizimu ndi za mdierekezi. Ife tikudziwa zimenezo. Ndipo ndi momwe, inu mumayenera kuyang'anira. Monga iwo . . .

³⁰ Chifukwa chomwe iwo anamutcha Yesu “Bezebule,” “mdierekezi,” chifukwa, inu mukuwona, Iye amakhoza kuzindikira maganizo a malingaliro awo. Mwaona, koma Iye anali Mawu a Mulungu. Ndipo Ahebrai 4 anati, “Mawu a Mulungu, akuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, ngakhale ozindikira malingaliro a mkati mwa mtima, malingaliro.” Mukuona? Chotero, Iye anali Mawu, Iye ndiye Mawu amoyo, ndipo Mawu amoyo amabwera mwa ife ndiyeno Iwo amadzachita mphamvu yomweyo pa ife. Mwaona, chimodzimodzi, chifukwa Iwo ndi Mawu omwewo. Mwaona, Ndi chinthu chomwe chomwecho pakati pathu. Ndipo njira yake ndi imeneyo. Ndipo nthawizina iwo omwe sali

mkatikati mwa zimenezo amalankhula ndi malirime, ndipo wina amatanthauzira iwo. Ndi chiyani chimenecho? Mawu kusandulika thupi pakati pathu.

³¹ Ndipo kenako, ife tikuzindikira ndiye kuti mngelo uyu adzalandira... mngelo wa m'badwo wa mpingo amene analandira "mwala." Iwo unali mwala *woyera*, kutanthauza kuti osati chilungamo chake, koma "chilungamo cha Mulungu Mwiniwake."

³² Ndipo mu mwala uwu munali "dzina," dzina lomwe panalibe amene amalidziwa koma iyeyo amene analandira ilo iyeyekha. Iye ankalidziwa ilo, koma panalibe wina aliyense akanakhoza kulidziwa ilo koma iye. Chotero pamene inu muwamva anyamata awa akukukomedwetsani inu, akunena awo; iwo ndi "John," iwo ndi "Paul," iwo ndi "Mary," iwo ndi "*ichi*," "*icho*," kapena "*chinacho*." Inu musazikhulupirire zimenezo, chifukwa ngati izo zikanakhala chomwecho, iye sibwenzi atanena chirichonse chokhudza ilo. Mukuona? Ndiko kulondola. Iye ayenera kulisunga ilo kwa iyemwini. Iye ankalidziwa. Panalibe amene ankadziwa koma iyemwini, koma iye ankalidziwa chifukwa wogonjetsa wangwiro aliyense amalandira dzina latsopano mwa—mwa—mwanjira imeneyo.

³³ Kodi inu munazindikira Abrahamu ankatchedwa Abram, koma pamene Mulungu anapita kuti akamugwiritse iye ntchito, Iye anamusintha dzina lake kudzakhala "Abrahamu." S-a-r-r-a anali Sarra, koma pamene Mulungu ankapita kuti akamugwiritse iye ntchito, Iye anamusintha dzina kukhala S-a-r-r-a-h: *Sarah*, "mfumukazi." Kodi inu mukudziwa kuti Yakobo...? *Yakobo* anali "wolanda." *Esau* amatanthauza "wofiira," waubweya ndi wofiira; wamutu wofiira, ndi wofiiraponsepense, anali Esau. Tsopano, ndipo *Yakobo* anali "wolanda." Ndipo *wolanda* ndi "wonyenga." Kodi Esau sananene kuti, "Kodi dzina lake silimatchedwa *Yakobo*, 'wolanda'?" Koma pamene iye anadzalimbana ndi Ambuye usiku wonse, ndipo nkupambana, ndipo nkudalitsidwa, Mulungu anamusintha dzina lake; *Yakobo* anadzakhala *Israeli*, "kalonga ndi Mulungu." Paulo ankatchedwa *Saulo* kufikira pamene iye anadzakumana ndi Mzimu Woyera mmawonekedwe a Kuwala komwe kunadzawalira pansu pa iye, dzina lake linasinthidwa kuchoka ku Saulo kudzakhala "Paulo." Simoni, pamene iye anadzakumana ndi Yesu, Iye anamusintha dzina lake kukhala "Petro." Icho...

³⁴ Ndipo pamene Yesu anagonjetsa, Dzina Lake linasinthidwa. Ndipo Iye amakhoza kuwulula Dzina limenelo, "Iye amene adzakhale ndi Iye, agonjetse monga Iye anachitira, iye analandira dzina latsopano; ndipo Ine ndidzawulula Dzina Langa latsopano kwa iye." Mukuona? Ndipo wogonjetsa aliyense, ine ndikutanthauza, pakati pa oterowo: atsoholeri amenewo ndi ena otero. Tsopano, ana onse a Israeli sanasinthe

maina awo, zoonadi. Uko nkulondola. Koma atsogoleri apamwamba amenewo, pamene iwo anagonjetsa, iwo analandira dzina latsopano. Mukuwona momwe izo zikulumikizirana mkati? Mwangwiro basi.

³⁵ Ndipo tsopano ife tikupeza kuti iye analinso ndi “mana obisika.” Tsopano, mana obisika amaimiridwa ndi mkate wopanda chotupitsa. Mkate wopanda chotupitsa unali wa ansembe okha. Uko nkulondola. Mkate wopanda chotupitsa unali wa ansembe okha. Ndipo iwo. . . Iwo umakhala chinthu chapadera chopangidwira wansembe, ndiye kuti, atsogoleri; ndipo munthu uyu amagonjetsa. Msokhano wonse umalandira mana, koma iye amalandira *obisika* (apadera) *mana*, kapena “*vumbulutso lapadera*,” oh, la yemwe Yesu anali, nanga bwanji Iyeyo, zonse za Iye. Mwaona, iye amalandira vumbulutso limenelo ngati iye agonjetsa. Kwa mngelo, “Gwiritsitsani, pakuti iye amene. . .” Iye anali atagonjetsa. Amalemba kwa *mngelo* wa mpingo. Mukuona?

³⁶ Tsopano ife tikupeza ndiye, usikuuno, ife tikuyambapo:

. . . kwa *mngelo wa mpingo wa Tiyatira lemba; zinthu Izi anena Mwana wa Mulungu, amene ali. . . maso ngati. . . malawi a moto, ndi mapazi ake. . . ngati mkuwa wonyezimira;*

³⁷ Tsopano, pamene ife tinamuwona Iye mu woyamba, M’badwo wa Efeso, kapena mu kuyamba kwa Chivumbulutso, ife tinamuwona Iye mu umunthu Wake wofutukuka pasanu ndi pawiri wa umunthu. “Tsitsi. . .” Ife tikupeza kuti Yohane anampeza Iye mu tsiku la Ambuye.

³⁸ Pamene Iye azibwera tsopano, Iye ndi Wansembe. Pamene Iye anali kuno padziko lapansi, Iye anali Mneneri, Mneneri wa Mulungu. Tsopano Iye anatenga Magazi Ake Omwe ndipo anapita patsogolo pa Atate, zomwe zikumupanga Iye Wansembe. Pamene Iye azibwereranso Iye adzakhala Mfumu. Mneneri, Wansembe, ndi Mfumu. Iye anali Mneneri wa Mulungu, Iye anali Mphungu. Iye anali Wansembe wa Mulungu, Iye anali Mwanawankhosa. Pamene Iye azibwereranso, Iye adzakhala Mkango, Mfumu, (fuko la Yuda) kuti adzalamulire.

³⁹ Koma pakati pa ntchito Yake ya Unsembe, pamene kachisi akusiyidwa, ndiye ife tikumupeza Iye ataima pamenepo. Ndipo Yohane anati iye anali mu Mzimu pa “Tsiku la Ambuye”; osati tsiku la chiseveni, osati Lamlungu, zonsezo ndi zolakwika. Ife tinazipeza zimenezo, tinazifufuza zimenezo kudutsa mu Lemba, ilo linali tsiku la Ambuye. Lero ndi tsiku la munthu. Kubwera kwa Ambuye kudzakhala tsiku Lake.

⁴⁰ Ndipo ife tikumupeza iye mu tsiku la Ambuye. Ndipo, pamene iye anawawona Ambuye, Iye anali atavala “tsitsi loyera ngati chipale.” Ndipo ife tikudziwa kuti izo zikuimira woweruza.

41 Chinthu china, Iye sanali Wansembe pamenepo, chifukwa Wansembeyo anali atazimangirira mozungulira pakati, kutanthauza *utumiki*. Koma Iye anali atazimangirira mozungulira pachidali, pamwamba *apa*, zomwe zinkatanthauza kuti Iye anali *Woweruza*. Ameni! Ndipo ife tinamuwona Iye akuyenda pakati pa zoyikapo nyali seveni zagolide.

42 Ndipo tsopano ife tinabwereranso ku “Wamasiku Amakedzana,” kukhala *woyera* pa Mpando Wachifumu Wachiweruzo pamene Daniele anamuwona Iye, “Anabwera kwa Wamasiku Amakedzana Yemwe tsitsi lake linali loyera ngati chipale.”

43 Tsopano, “zoyera.” Oweruza Achingerezi akale kudutsa mzaka, anakonda kukhala, pamene iwo apita ku mpando wachiweruzo iwo amakavala wigi yayikulu yoyera, wigi yoyera-mwachipale, chifukwa iwo anali oweruza. Ndipo Yohane anamuwona Iye mu tsiku la Ambuye, pamene Iye anali Woweruza. Ameni!

44 Tsopano ife tikupeza kuti “Iye anali nawo maso ngati malawi amoto.” Maso amenewo ndiye ngati lawi la moto. . . Nthawi ina maso amenewo anachita mdima ndi misozi yaumunthu. Iwo amatha kuimirira ndi kulira pa munthu amene akufa, ndipo akudziwa kuti mmaminiti asanu otsatira iye adzakhala ali moyo kenanso; koma basi chisoni cha umunthu. Koma kuseri kwa zimenezo kunali mphamvu yoteroyo kuti Iye amakhoza kuyang’ana kupyozza mmoyo wa munthu ndi kumuuzza iye yemwe iye anali ndi zonse zokhudza izo. Chifukwa izo zinali kubwera tsopano mu chinyezimiro ichi ngati moto. Maso akhoza kuyang’ana uku ndi uku kudutsa padziko lapansi, ndi kuwona chirichonse chimene chikuchitika. Kodi inu mudzakaima pati pa Tsiku la Chiweruzo? Machimo anu adzakhala pa mbalambanda pamaso pa Iye.

45 Ndipo inu mukuzindikira kuti Iye anali, “Kuchokera mkamwa Mwake, lu—lupanga lakuthwa konsekonse,” chimene ife tinachipeza kuti anali *Mawu*.

46 Ife tinawona mapazi Ake anali “mkuwa woyengeka,” ndi zina zotero, zomwe zimatanthauza “maziko Ake.” Iye amaponda moponderamo mphesa mwa mkwiyo wa Mulungu Wamphamvuzonse, ndipo anapondereza pansu ndipo anatenga tchimo pa Iye, ndipo anatuluka kunja, ndipo anamsangalatsa Mulungu. Zoonso zimenezo. Ndipo maziko Ake ndiwo maziko athu:

Pa Khristu, Thanthwe lolimba, ine ndaima,
(anatero Eddie Perronet.)
Maziko ena onse ndi mchenga wotitimira. (Uko
nkulondola.)

47 Tsopano ife tikupeza apa, nthawi iliyonse pamene Iye akumana ndi m’badwo wa mpingo, Iye amamulankhula

iyе ngati mmodzi wa Maina Ake Aumulungu. Tsopano ife tikupeza mmbuyo uko, woyamba mmavumbulutso onse ndi Umulungu (Umulungu Wapamwamba) wa Yesu Khristu: “Ine ndine Iye amene anali, amene ali, amene adzabwera. Ine ndine woyamba, ndi womaliza, Mulungu Wamphamvuzonse.” Mwaona, vumbulutso loyamba. Yohane anapotoloka kuti ayang’ane chomwe chimayankhula ndi iye. Chinthu choyamba, Iye anamuyankhula iye pa . . .

⁴⁸ Mfumu iliyonse, pamene iyo ikuyankhulidwa, iye—iye—iye amanena yemwe iye ali; aliyense. “Ndine *Wakuti-ndi-wakuti* ine ndikamayankhula ndi inu, inu simukundidziwa ine. Ndine William Branham, ndine *John Doe*,” aliyense amene ali.

⁴⁹ Iye anati, “Ine ndine woyamba ndi wotsiriza; Iye amene anali wamoyo ndipo ndi wakufa; ndi wamoyo kwanthawizonse.” Oh, mai! Umulungu. Apa ife tikumuwona Iye mu umunthu Wake wofutukuka pasanu ndi pawiri wa chikhalidwe Chake cha ulemelero. Mu m’badwo wa mpingo uliwonse Iye—Iye akuwafikira iwo mu umulungu wosiyanasiyana wa maumulungu amenewo, osiyanasiyana a magawo a ulemelero amenewo.

⁵⁰ Tsopano, usikuuno, Iye akubwera ndi moto woyaka. Iye akuyang’ana pansu mu Laodikaya . . . kapena pansu mu Tiyatira. Uwu ndi m’badwo umene mpingo wakwatiwa ndi Chikatolika ndi chikunja, kapena Chinikolai ndi chikunja zinakwatirana pamodzi ndipo zinapanga ndi kubereka mpingo woyamba, mpingo wa chibungwe.

⁵¹ Ndipo Mulungu ananena kuti *ntchito* za Chinikolai (zomwe zinali mu Efeso), uko mu—mpingo wawung’ono wa Pergamo zinadzakhala “chiphunzitsa,” ndipo anati icho chinali “chiphunzitsa cha Balamu.” Ndipo Balamu anali yemwe anaphunzitsa Israeli kuti apite kumeneko ndi kukachita ziwerewere, kapena iwo anakachita zachiwerewere ndi Moabu (yemwe anali membala wofunda wa mpingo), kapena mpingo wa wamba, bungwe lalikulu. Ndipo ife tikupeza kuti Mulungu anati, chiphunzitsa cha Chinikolai chimenecho chimene chinali . . . kutenga . . . kuika mphamvu zonse mu mpingo ndipo nkuika pambali ndi kuwupanga iwo kukhala bungwe, Iye anati, “Inu mumadana nazo izo, ndipo Inenso ndikudana nazo izo.” Iye akungopitiriza kumanena kuti, “Ndikudana nazo! Ndikudana nazo! Ndikudana nazo!” Ndipo izo zafika pachimake *apa*. Taonani momwe mpingo unafinyidwira kunjа, pomwepa *apa* mpaka nkungokhala kanthu kakang’ono chabe, ndipo ndiwo mpingo womwe tikukhalamo tsopano.

⁵² Tsopano, mu tsiku ili limene vumbulutso ili linabwera, kapena linali ku mpingo uwu, ilo linali tsiku limene Roma anali atamanga pa miyala yayikulu ya malo awo, a udzu ndi tsekela. Koma Iye akuyankhula ndi mpingo uwu kuti “Iye adakalibe moto woyaka womwe umayang’ana pansu kudutsa nthawi,

ndipo maziko Ake si udzu, ziputu, koma ndi mkuwa wolimba, woyesedwa mu ng'anjo ya moto." Maziko ake ndi wotsimikizika. Ine ndikuzikonda zimenezo. Ife tikudziwa pomwe ife taima.

53 Chabwino:

Ine ndikudziwa ntchito zako, ndi chikondi chako, ndi ntchito yako, ndi chikhulupiro, ndi chipiro chako, ndi ntchito zako; ndipo zomaliza—zomaliza zidzakhala zochuluka kuposa zoyamba.

54 Chabwino, mpingo ukuwoneka kuti watsala pang'ono kuti udulidwe kwathunthu, kungofota pang'ono basi, ndipo iwo anali atachoka pa misonkhano yayikulu yauzimu, ndipo amakhala ngati amadalira pa ntchito. Mulungu samafuna kuti ife tizidalira ntchito.

55 Ndicho chi—chizindikiro cha bungwe. "Ife timamutenga Abiti Jones chifukwa cha mtengo wina. Ndipo ife timamutenga *Wakuti-ndi-wakuti*, ana awo, chifukwa cha zovala zina." Ndipo zonsezo nzabwino. Koma, inu musamadalire pa zimenezo, inu musamachite zimenezo. M'bale, izo—izo—ndi ntchito zabwino; nzika yabwino, yamakhalidwe abwino imachita zimenezo. Koma zomwe zimatengera kuti ukhale Mkristu ndi chokuchitikira chobadwanso mwatsopano, ubatizo wa Mzimu Woyera. Chabwino.

56 Anafota, iwo anasankha kuti azichita ntchito mmalo mwa chikondi ndi chikhulupiro, kumatenga zochuluka ndi zochuluka nthawi zonse pamene zimapitirira.

57 Chabwino:

Ine ndikudziwa ntchito zako, . . . Ine ndikudziwa chikhulupiro chako, ine ndikudziwa chipiro chako, ndi zina zotero . . .

58 Koma tsopano ife titenga ndime ya 20, mvetsarani ku izi:

Komabe ine ndiri nazo zinthu pang'ono zokutsutsa iwe, chifukwa iwe ukulola mkazi uja Yezebeli, amene amadzitchula yekha mneneri wamkazi, kuti aziphunzitsa ndi . . . kunyenga atumiki anga ndi kuchita ziwerewere, ndi kudya zinthu zoperekedwa nsembe kwa mafano.

59 Tsopano, "mkazi." Kodi ife tinapeza kuti *mkazi* amaimira chiyani usiku wathawu? A "mpingo." Tsopano, tsopano ife tikupeza apa kuti iwo amatchedwa "Achinikolai," "chiphunzitsa cha Balamu," ndipo tsopano zafika kwa "Yezebeli."

60 Tsopano, "Yezebeli." Ngati inu mungazindikire, iyi ndi mbiriyakale yopambana. Tsopano, ngati inu mukufuna kulemba izo, muyambire mu Mafumu Woyamba, pafupifupi . . . Mafumu Woyamba, pafupifupi 16. Yezebeli sanali mwana wamkazi wa Abrahamu; ngakhalenso gulu ili apa, Roma wachikunja. Achinikolai anali gulu lozizira, lofunda la Akristu omwe

anadzipatula okha kwa Akhristu enieni, “ankawoneka opanda Chikhulupiriro.” Ndipo iwo ankafuna kuwupanga mpingo kukhala ngati loji, chimodzimodzi monga iwo ali nazo lero; ngati loji, wopanda Mzimu mmenemo nkomwe; “Masiku a zozizwitsa anapita. Izo zonse zinali za m’badwo wina. Ife tiri nawo ubale.” Mmisiri wabwino, Munthu Wosamvetsetseka, kapena chirichonse chonga chimenecho chimabala zimenezo. Ndipo izo ndizabwino, koma zimenezo sizidzatenga konse malo a kubadwa kwatsopano mwa Yesu Khristu, chipulumutso ku moyo, Choonadi ichi.

⁶¹ Chabwino, Yezebeli uyu. Tsopano iye anali mwana wamkazi wa Abrahamu, izo nzoona, mfumukazi ya wopembedza mafano. Pa nthawi imeneyo pamene banja lachifumu, banja lake lachifumu, linkadziwika ndi kukhulupirika kwa nkhanza kwa uburutu kwa Baala. Abambo ake anali ansembe a fano la A-s-t-a-r-t-e (Ine sindikudziwa momwe inu mumatchulira, ine ndinangozitenga izo mu mbiriyakake). Ahabu anagwiritsa ntchito kachitidwe kake monga Konstantini. Fuko lamphamvu lapamwamba ili linali pafupi ndi Israeli, chotero mwakuti . . .

⁶² Kodi Konstantini anachita chiyani usiku watha uja? Iye anali asanatembenuke. Iye anali wandale. Kodi iye amayesetsa kuti achite chiyani? Iye anawatenga Akhristu, pamene iwo anamuuzwa iye kuti iwo anali atapemphera . . . (Ndipo tsopano pamenepo, kumbukirani, iye ndi- . . . ife tikuyankhula tsopano za Chinikolai). Ndipo iye anati ngati iwo angapemphere, ndipo iye nkupambana nkondo iyi, ndiye iye adzakhoza—iye akanadzakhala Mkhristu. Iye anali ndi loto. Anapenta zishango zake kukhala zoyera, usiku womwewo, za mtanda. Komwe Alupanga a Columbus anabadwa, pa nthawi yomweyo; tsopano apo ndi pomwe iwo amatengapo maimidwe awo. Koma iye sanachitepo chirichonse ngati Mkhristu! Pa umodzi wa mipingo ya Chinikolai, wotchedwa St. Sophia, iye anayikapo mtanda. Monga ine ndinanenera usiku watha, ndicho chinthu chokhacho chimene iye anachita chimene chinamveka ngati iye anali wa mpingo, momwe ine ndikanakhoza konse kukunkhira kuchokera mu lirilonse la masamba a mbirizakale; ndi ophunzira ena ambiri amanena chinthu chomwecho. Ife sitikudziwa kalikonse zokhudza kutembenuka kwake, tsopano. Koma kodi iye analowa mu chiyani? Chinthu chimene iye ankafuna kuti achite, iye anawona wochuluka wa Roma, tsopano.

⁶³ Tsopano tayang’anani izi, penyani kachitidwe aka. Ndipo penyani momwe Baibulo limatsimikizira izo, Mulungu, mazana ndi mazana a zaka izo zisanachitike. Ndipo Konstantini anagwiritsa ntchito kachitidwe komweko, Mulungu ananena apa, komwe Ahabu anagwiritsa ntchito.

⁶⁴ Tsopano, Konstantini anawona gawo lalikulu la anthu ake anali Achinikolai awa, Akhristu. Ena a iwo ankatchedwa “ampatuko,” ndiwo Achipentekoste; iwo anali “ampatuko

ndi oyera-odzigudubuza,” ndi zina-zambiri. Apo ndi pamene zizindikiro zanu zenizeni ndi zodabwitsa zinaikidwapo. Koma mpingo *wachithupi* ndiye unali ukubwera kudzakhala bungwe. Kodi iye anachita chiyani? Konstantini anasewera gawo lochenjera. Iye anapita kumeneko ndipo anakatenga abwenzi ake achikunja, ndipo anakatenganso abwenzi ake Achikhristu, ndipo analumikizitsa mipingo palimodzi, anakhazikitsa a— a... anachibweretsa chikunja mu Chikhristu. Chikhristu ndi chikunja zinakwatirana mu mpingo wa Pergamo.

⁶⁵ Tsopano, kodi Iye ananena chiyani apa za usikuuno? Chinthu chomwe chomwecho chimene Ahabu anachita. Ahabu, kuti alimbikitse ufumu wake, anakwatira Yezebeli, wopembedza mafano uyu; kuti alimbikitse ufumu wake, kuti akhale ndi mphamvu zambiri mu Israeli.

⁶⁶ Ndipo ndizo zomwe mipingo ikuyesetsa. Inu mukuwona kumene iwo akuyesetsa kuti apange Baibulo, likhale litatuluka pofika chaka chamawa mu '62? Akuti ndi Baibulo lomwe lidzawasangalatse Ayuda, ilo lidzawasangalatsa Akatolika, ndi kudzawasangalatsa Achiprotestanti. Oh, m'bale! Ine ndiri ndikodula ka nyuzipepala. Ine sindinakatenge iko usikuuno, inu munandimva ine ndikuwerenga izo usiku wina uja. Ndi zimenezotu, inu mwaona.

⁶⁷ Oh, zinthu zimenezo kuyesetsa kuti achulukane! Iwo amatenga zinthu zopatulika za Mulungu ndi kuzimwaza izo mulimonse, kuti awonjezere ndi kupanga manambala ambiri. Ndi chimene mpingo wachita. Iwo unawalandira anthu kuti alowe mu zimenezo pa maziko a kugwirana chanza, ndipo unatengeramo zigawenga ndi china chirichonse, anthu osatembenuka. Koma mu Thupi loona la Khristu, lomwe siliri bungwe, koma lachinsinsi—Thupi lanthano la Khristu, inu mukhoza kungolowa mmenemo mwanjira imodzi, ndipo ndiyo kudzera mu ubatizo wa Mzimu Woyera. Kulondola! Ndipo zizindikiro zomwezo zomwe zinawakantha atumwi amenewo, zikuwukantha Mpingo. Ndiko kulondola ndendende!

⁶⁸ Tsopano, ife sitikusowa kuti tizinyengerera ndi kuti, “Chabwino, ife tipita ndi kukajowinana ndi Assemblies. Ife tipita tikajowinane ndi a Umodzi. Ife tipita kukajowinana ndi *awa*, kapena Abaptisti, kapena Amethodisti.” Tiyeni tijowinane ndi Khristu! Tikhale amfulu kwa zinthu izi. Chifukwa lililonse la mabungwe amenewo ndi abwino bwino, koma iwo—iwo amatenga ziphunzitso zawo ndi zinthu zawo, ndipo iwe umayenera kupita kukawona ngati woyang'anira wamkulu angakuloleze iwe kuti ubwere mu dziko limenelo ndi kudzakhala ndi msonkhano. Ngati iwe sukuphunzitsa ndendende basi monga momwe iwo amachitira, akutulutsira iwe panja, iwe sungakhale ndi Baibulo. Mulungu sangakhoze kuchita zimenezo, Iye amadana nazo izo. Mkristu wina aliyense wobadwanso mwatsopano angatero nayenso. Ambiri a anthu

awo kunja uko mwamtheradi... amafuna azitero, amafuna azitumikira, ndipo amafuna azikhala ndi chiyanjano. Koma inu simungachite zimenezo, iwo akhoza kukutulutsani panja. Chabwino, asiye ni iwo akutulutseni inu panja, kazipitirirani, kalandireni Mzimu Woyera mulimonse. Ndizo ndendende kulondola. Koma, inu mukuwona, iwo—iwo amafuna kuti amvetse zimenezo—chiphunzitsa chimenecho. Iwo amafuna kukutenga iwe pomwe uli ndi ndalama zambiri. Abaptisti anali ndi mbalume mu '44, "Ochuluka miliyoni mu '44." Kodi iwo anapeza chiyani?

⁶⁹ Chimodzimodzi monga mlaliki wamkulu Billy Graham ananena, pamene iye anali mu Louisville, "Ine ndikapita mu mzinda..." Anati, "Paulo Woyera akapita mu mzinda, iye amakantembenuza mmodzi; akabwererako chaka chotsatira iye— amakakhala ndi sarte kuchokera pa mmodzi uja; zidzukululu-zidzikululu-zidzukululu-zidzukululu-zidzukululu-zidzukululu, kuchokera pa kutembenuka kumodzi kumeneko." Iye anati, "Ine ndikapita mu mzinda, ndikakawaitanako sarte sauzande, ndikamadzabwereranso chaka chotsatira ndipo sindimakapezako sarte." Ndipo zomwe iye ananena, iye—iye anapanga neno labwino, komabe ine sindikukhulupirira kuti m'bale wathu wofunikayu amalondola. Iye anati, "Inu alaliki aulesi." Anati, "Ine ndikakupatsani inu maina awo ndi adiresi, inu mumakhala ndi mapazi anu pamwamba pa desiki ndi kumawalembera iwo kalata mmalo mopitako, ndi kukayankhula nawo iwo."

⁷⁰ Ine—ine ndinakhala ngati ndinamuyamikira iye chifukwa cha chimenecho. Ine ndimakonda munthu azikhala chimene iye ali, osati wachinyengo; kuima powonekera ndi kukhala chimene iwe uli. Ndipo ine ndimazikonda zimenezo. Koma ine ndikufuna kunena kuti, "Billy, ndi ndani anapita kumeneko kuti akamutenge wotembenuka uja yemwe Paulo anamutembenuza? Chimene izo chinali, Billy, ngati iwe utangosiya zomawalola iwo kumapita kumeneko ndi kumakagwirana chanza, ndi kudzukapo, ndi kuti, 'Inde, ine ndamulandira Yesu kukhala Mpulumutsi wanga,' ndi kumusiya iye akhale pamenepo kufikira atafa ndi kuvunda, ndipo wabadwanso mwa Mzimu Woyera, iye akapanga otembenuka atsopano."

⁷¹ M'bale, ndiwe... iye amatumphuka ndi moto, iwe sungakhoze kumuzimitsa iye. Iye amakhala ngati nyumba yoyaka moto mu mphepo yaikulu, inu simungakhoze basi kuchita zimenezo. Oh, iye akufalitsa konsekonse, m'bale, wotembenuka weniweni wa Khristu, iye sangakhale chete. Iye amakhala basi... iye amakhala akuyenda. Oh, ndine wokondwa kwambiri! Oh, mai! Ubatizo wachikale wa Mzimu Woyera umene umayatsa solo moto! Sungakhoze kungokhala phee, mphepo ikukukupiza iwe, mphepo ya nkokomo wamphamvu imangopitirirabe kumakuwomba iwe.

Bwanji ine ndimangopitirizabe kumasonkhezera nkhuhi, ndi kumapitirirabe chitsogolo. Inde, bwana! Panalibe amene amamutenga womtembenusa Paulo, Paulo amawatengera iwo mozama kwambiri mwa Khristu kufikira iye amafa kwa iyemwini, ndipo amakhala wamoyo mwa Khristu, ndipo Iye amachita zina zonsezo. Ndiko kulondola! Ndizo zomwe izo ziri.

⁷² Abale a Baptisti ndi abwino bwino. Koma milioni enaso, kodi izo zimachita ubwino wanji? Inu muli nawo mayina ena miliyoni. Chabwino, mungokhala pansi ndipo mupange ena ngati inu mukufuna kukawayika iwo kumeneko. Izo nzabwino, koma, m'bale, zomwe ife tikufuna ndi maina pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa, wophedwa chikhazikitsireni maziko a dziko lapansi, wotsukidwa m'Magazi, wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, zizindikiro ndi zodabwitsa zikukutsatirani inu.

⁷³ Fufuzani mbirizakale. Ine ndikadakonda inu nonse mukanatenga ma Nicene Councils ndi kukawerenga zinthu zimenezo, kuti mukawone momwe ofera amenewo amagwirizira lawi ilo la pentekoste. Ine ndikuuzani inu tsopano, m'bale, inu a Baptisti, Methodisti, ndi chirichonse chimene inu muli, Kuwala kooka kwenikweni... si bungwe la Chipentekoste, tsopano; koma Kuwala kowona, kwenikweni ndi Chokuchitikira cha Chipentekoste. Pansi... Ine ndakhala masiku ndi masiku tsopano, mbirizakale zimenezo, ndakumbamo mmenemo zonse zimene ndikanazipeza paliponse, ndipo ndi lawi la pentekoste limenelo limene linatsala lamoyo kuyambira pa Pentekoste mpaka nthawi ino. Inde, bwana! Lakhala likuthamangitsidwira panja.

⁷⁴ Ena a iwo amati, “Chabwino, mpingo wawukulu wa Katolika wapirira mafunde. Bwanji, izo zikutsimikizira kuti iwo ndi Mpingo weniweni.” Bwanji, sichinthu chachirendo kwa ine, ndi boma ndi zina zonse kumbuyo kwake, iwo ukhoza kumakhalapo. Koma ndi chiyani—chodabwitsa ndi chiyani, ndi gulu laling'ono lija limene linachokapo, ochepa apang'ono aja, anathamangitsidwira panja, anaponyedwa mu ndende, anachekedwa mziidutswa. Kodi zinatheka bwanji kuti anakhalapobe? Chifukwa Mzimu wa Mulungu wamoyo umayendayenda mu umunthu wawo. Ndipo ziwanda zonse za ku gehena sizingawugonjetse Iwo! “Pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizidzawulaka Iwo.” Ndi chimenecho chinthu chenichenicho. Ndi chimene chinapereka Mzimu Woyera kwa alaliki Achimethodisti awa, ndi zina zotero, apa. Mwaona, iwo umawapangitsa iwo kumadzukapo, umachita chinachake kwa inu. Izo sizidzalephera konse.

⁷⁵ Ahabu, wachinyengo uja. Mwaona, iye akupita, iye akuti, “Tsopano, ngati ine nditangokwanitsa kuti ndikhazikike tsopano, ndi kutenga fuko lalikulu ili. Ndipo ngati ine nditakwatira mwana wamkazi wa mnyamata wachikulire uyo

kumusi uko, chabwino, izo...ife—ife tidzakhala abwenzi.” Kodi iye amachita chiyani? Amagulitsa maufulu ake omwe akubadwa.

⁷⁶ Tsopano, pamene mpingo uwu wa Chiprotestanti *udzabwerera* mmbuyo ndi kukalumikizana ndi mpingo wa Katolika, iwo udzachita chinthu chomwecho unachita mmbuyo uko. Ahabu anakhala mu tsiku limene . . .

⁷⁷ Izo zakhala katatu. Iye anali pakati pausiku paulendo waku Israeli, ndipo *apa* zinafika pakati pausiku kachiwiri, ndipo ife tafika pakati pausiku kachiwiri *apa*. Mibadwo itatu izi zisanati; analowa mkati *munu*, mkati *umu*, ndi mkati *umu*.

⁷⁸ Tsopano, ngati inu mungazindikire, Ahabu anakwatira Yezebeli kuti alimbikitse anthu ake. Ndizo ndendende zomwe Konstantini anachita. Iye anakhazikitsa mpingo waukulu kwambiri, ndipo anatenga guwa ndipo anapanga nsangalabwi yaikulu, anamuveka munthu uyu, papa, anamukhazika iye pamenepo. Iye anali mulungu wamoyo, iye amakhoza kuyankhula nawo, ndi—ndi kumuuzza iye za machimo awo, ndipo zimenezo zinangokondweretsa mpingo wakale wofunda uwo, ndipo anapita kutali. Ndithudi! Ndi zimenezotu! Chabwino, koma zimenezo sizinamusangalatse munthu uyo amene anabadwanso kachiwiri, pamene iwo anatenga zimenezo ndipo kenako nkubweretsamo miyambo yachikunja yonenera mapemphero. Kodi iwo anachita chiyani? Iwo anamutsitsapo Jupiter, ndipo anamuikapo Petro. Iwo anamutsitsapo Venus, ndi kumuyikapo Maria. Ndipo izo zinabweretsa—izo zinabweretsa chikunja mmagulu Achikhristu.

⁷⁹ Ndipo pamene Ahabu anakwatira Yezebeli, iye anachita chinthu chomwe chomwecho. Iye anabweretsa kupembedza mafano mu Israeli. Ndipo kodi Yezebeli anachita chiyani? Iye anapha mneneri aliyense yemwe iye akanakhoza kuyikapo manja ake. Nkulondola uko? Momwemonso anachita mapapa. Mkhristu wona aliyense yemwe iwo akanakhoza kumugwira, iwo anawapha iwo.

⁸⁰ Koma kunali nyenyezi ya m’badwo umenewo, Eliya wokalamba! Oh, inde, bwana! Iye sanachite mantha, kuwauza iwo za zimenezo. Inde, bwana! Iye anali nyenyezi ya Mulungu ya m’badwo *umenewo*. Anafika nthawi ina iye anati, “Ambuye, ndatsala ndekha ndekha.”

⁸¹ Mulungu anati, “Tsopano, dikira miniti, dikira miniti, dikira miniti, Eliya.” Uh-huh. “Ine ndiri nawo seveni handiredi ndawabisa pozungulira, kutsidyako. Mukuona? Iwe sukudziwa kumene iwo ali. Iwo ali kunja uko, Afarisi, Asaduki, Abaptisti, Amethodisti, ndi Apresbateria, koma ine—ine ndikawatulutsako iwo kumeneko, iwe ungodikira. Mukuona? Ine ndiri nawo iwo kunja uko. Alipo . . . iwo ali—iwo ali—iwo ndi Anga, ndipo iwo sakugwadira Baala panobe.” Koma Eliya wokalambayo anali

Liwu la Mulungu mu tsiku limenelo. Iye ndithudi anali woimira kumene wa Liwu la Mulungu pa kudza koyamba kwa Khristu, ndipo izo zidzakhala mtundu wa Liwu pakubweranso kwa Khristu kachiwiri, malingana ndi Malemba.

⁸² Tsopano, ife tikupeza kuti Yezebeli wamng'ono uyu, pamene iye anakafika kumeneko, iye anali wakuti akaphwasula kwenikweni maguwa onse a Mulungu ndi kukamangapo maguwa ake ake. Ndipo iye anawapangitsa Aisraeli kuti azigwadira fano. Ndizo ndendende zomwe Konstantini anachita pamene iye anayambitsa mpingo wa Katolika. Iye anabweretsa chikunja mu—mu mpingo wa Chikhristu, ndipo anawapangitsa Akhristu kuti azigwadira mafano. Ndizo ndendende m'badwo wa mdima kachiwiri; m'badwo wa mdima wa Israeli, m'badwo wa mdima wa—wa mpingo; kugwadira mafano. Ndipo Eliya anali nyenyezi mu tsiku lake.

⁸³ Ndipo anapangitsa Israeli yense kupembedza Baala, ndipo chomwechonso unachita mpingo wa Katolika ku Tiyatira.

⁸⁴ Tsopano, ine ndikufuna kuti inu muzindikire chinthu china chokhuza apa, ine ndimatenga mbiriyakale yanga apa. Yesu ananena kuti iye anali. . . ankadzitcha yekha mneneri wamkazi. “Mkazi uja Yezebeli, yemwe amadzitcha yekha (amadzitcha yekha) mneneri wamkazi.” Tsopano, inu mukuona, mpingo wa Katolika sumalola anthu awo kuti aziwerenga Baibulo chifukwa iwo amanena kuti wansembe ndiye yekhayo amene angathe kuzindikira Mwauzimu Mawu amenewo.

⁸⁵ Chabwino, uko ndi kutanthauzira kowona kwa mneneri. Mneneri amakhala ndi Kutanthauzira Kwauzimu kwa Mawu a Mulungu. Ndiko kulondola ndendende. Munthu angamuthe bwanji wina, winawake, “mneneri” ndipo kenako nkuti, “iwo ali ndi vumbulutso lolakwika”? Izo ndizomveka mofanana monga umwana Wamuyaya, inu mwaona. Mukuona? Mwaona, ndi—ndizo. . . Mneneri amatanthauza “wozindikira wolondola, iye amene Mawu a Ambuye amabwerako, vumbulutso linabwera kwa iye.” Mawu akuti *mneneri* amatanthauza “wozindikira wa Mawu Aumulungu.” Yesu anati, “Ngati patakhalo mmodzi pakati panu amene ali wauzimu kapena mneneri, Ine Ambuye ndidzayankhula ndi iye. Ndipo ngati zomwe iye anena zidzachitika, ndiye mudzamumvere iye, Ine ndiri naye iye. Ngati izo sizichitika, ndiye musamumvere iye.” Ndizo zonse. Iwo anali—iwo anali Mawu Aumulungu a Mulungu, ndipo Mawu a Ambuye amadza kwa aneneri.

⁸⁶ Tsopano, iwo ananena kuti *mpingo* uwu panthawiyo unali “mneneri.” Tsopano kumbukirani, izo zasintha kuchokera ku Chinikolai tsopano, izo zasinthidwa kukhala “*iyē*.” Inu mukuziwona zimenezo? A “Yezebeli.” Tsopano, usiku wathawu zinali “chiphunzitso cha Balamu.” Mwaona, “chiphunzitso cha Chinikolai” ndi “chiphunzitso cha Balamu.”

⁸⁷ Tsopano, Balamu anali amene anachita ziwerewere ndi Israeli. Ndipo kodi anachita chiyani a—a—Achinikolai? Anapanga bungwe. Chotero muwayike awiri onsewo pamodzi ndipo inu mumupeza *iy*e, “mpingo.” Ndithudi! Chivumbulutso 17, “Hule lalikulu limene likukhala pa madzi ambiri.” Mkazi, wachiwerewere. Iye ndi ndani, kapena iye ndi wachiwerewere bwanji? Iye akuchita ziwerewere, ziwerewere zauzimu, kutanthauzira molakwika Mawu kwa anthu. Chokaniko ku zotengeka zoterozo! Ndizo kutengeka kwenikweni. Ndiko kulondola.

⁸⁸ Tsopano, onani, iye akudzitcha yekha mneneri wamkazi, “Ndife amenewo! Ndife bungwe! Ndife bungwe la Laodikaya aponso, bungwe la amuna, ndipo ife taganiza *izi*, ndi *izi*, ndi *izi*. Chotero inu muzimvetsera kwa ife!” Koma . . .

⁸⁹ Uyo—wansembe wamng’ono uja kumtunda kuno anadzandifunsa ine za Elizabeth Frazier, kapena mtsikana uja wa a Frazier. Anati, “Ka—kardinolo akufuna kuti adziwe ngati inu muti . . . kapena bishopu, ngati inu munamubatiza mtsikana wa a Frazier uyu.” Anati, “Iye akukhala Mkatolika.”

Ine ndinati, “Eya, ine ndamvetsedwa zimenezo.”

Anati, “Kodi—kodi inu munamubatiza iye?”

Ine ndinati, “Inde, bwana.”

Anati, “Inu munamubatiza chotani iye?”

Ine ndinati, “Mu ubatizo wa Chikristu.” Uh-huh.

Iye anati, “Chabwino, inu mukutanthauza chiyani pamene?”

Ine ndinati, “ubatizo wa Chikristu, momwe Baibulo limanenera. Pali njira imodzi yokha yobatizira mu ubatizo wa Chikristu. Munthu aliyense mu Baibulo ankamizidwa mmadzi mu Dzina la ‘Yesu Khristu.’”

⁹⁰ Iye analemba, anayambapo kumalemba monga choncho. Anati, “Inu mukudziwa, mpingo wa Katolika unkachita zimenezo.”

Ine ndinati, “Liti?” Ine ndinati, “Ine ndiri nazo mbirizakale zonse apa zomwe ine ndikanakhoza kuzipeza, kuchokera ku London ndi kwina kulikonse.” Kuchitira kuti ine ndikhoza kuweringa pamene ora ili liti lidzafike posachedwapa, pomwe chinachake chiti chidzachitike. Hmm. Ine ndinati, “Ine—ine ndikufuna kudziwa kuti ndi kuti.” Ine ndingapite . . .

Iye anati, “Oh,” iye anati, “mu Baibulo.”

Ine ndinati, “Kodi inu mumanena zimenezo . . .?”

Iye anati, “Yesu anawupanga bungwe mpingo wa Katolika.”

Ine ndinati, “Kodi Petro anali papa woyamba, ndiye?”

Anati, “Ziyenera ndithudi.”

Ine ndinati, “Ine ndimaganiza ‘mpingo ndi wosalephera ndipo siwumasintha, ndipo misa zonse zimanenedwa mu Chilatini kuchitira kuti iwo usasinthe.”

Iye anati, “Izo nzowona.”

⁹¹ Ine ndinati, “Chabwino, inu ndithudi mwasintha zina kuyambira nthawi imeneyo.” Ine ndinati, “Ngati Baibulo limenelo ndi bukhu la Katolika, ndiye kuti ndine Mkatolika wakachitidwe kachikale.” Mukuona? Uko nkulondola. Ine ndinati, “Ndine Mkatolika wakachitidwe kachikale, ndiye.” Ndipo ine ndinati, “Izo ndithudi zinali. . .”

Iye anati, “Chabwino, tsopano, inu mwaona, Baibulo ndi mbiriyakale chabe ya mpingo wa Katolika.” Iye anati, “Mulungu ali mu mpingo Wake.”

Ine ndinati, “Mulungu ali mu Mawu Ake.” Uko nkulondola.

⁹² “Mulole Mawu Anga akhale owona, ndipo mawu a munthu wina aliyense abodza.” Ndipo apa pa Bukhu ili la Chivumbulutso ndi Bukhu lokhalo (Ndiloreni ine ndibwereze izi.) limene Yesu anaikapo kuvomereza Kwake. Ndipo chinthu choyamba chimene Iye anachita chinali kuwulula Umulungu Wake, ndipo Iye amachita izo kwathunthu. Ndipo anati, “Aliyense amene adzachotsere kalikonse mwa Ilo kapena kudzawonjezera kalikonse kwa Ilo, zomwezo zidzachotsedwa (gawo lake) kuchoka mu Bukhu la Moyo. Wodala ali iye amene awerenga, kapena iye amene amva. Ndipo wotembereredwa ali iye amene adzawonjezera chinthu chimodzi kwa Ilo kapena kuchotsamo kalikonse kwa Ilo.” Ndi zimenezotu, chotero inu mukuliwona gawo lowopsyalo. Chotero musadzawonjezere konse kanthu kwa Ilo; ingolisiyani Ilo momwe Ilo liriri, ndipo muzingopitirira nazo.

⁹³ Mzimu udzaulula Ilo kwa inu ngati inu mungokhala odzichepetsa, mumufunse Iye. Mukuona? Uko nkulondola. Tsopano, chotero Ilo si lovuta. Mulungu . . . Yesu anawathokoza Atate chifukwa chakuti. . . anati, “Ine ndikukuthokozani Inu, Atate, kuti Inu munabisa zinthu izi kwa maso a aphunzitsi, ndi mabishopu, ndi makardinolo, oyang’anira onse, ndipo—ndipo mwaulula Izo kwa makanda omwe ati adzaphunzire.” Mukuona?

⁹⁴ Ndizo zimene inu mukufuna. Ndi vumbulutso la Mulungu limene likhoza kungobwera monga Iye ananenera kumeneko, “Kodi anthu amati ndine ndani?”

Iye anati, “Inu ndinu Khristu, Mwana wa Mulungu Wamoyo.”

⁹⁵ Iye anati, “Simoni, iwe sunaphunzire izo ku seminare. Mukuona? Palibe amene anakuwuzapo iwe zimenezo. Izo zinabwera, linali vumbulutso kuchokera Kumwamba. Ndipo pa thanthwe ili ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizidzawulaka Iwo.”

⁹⁶ Ndizo ndendende vumbulutso limene Abele anali nalo pachiyambi. Ndi vumbulutso; linali nthawi imeneyo, likadali vumbulutso, ndipo lidzakhala vumbulutso nthawi zonse. Uko nkulondola.

⁹⁷ Tsopano, ife tikupeza apa kuti iye anali mkazi tsopano, ndipo *mkazi* amaaimira “mpingo.” (Nkulondola uko? Khristu akudzera chiyani? Mkwatibwi, mkazi, namwali wosakhudzidwa.) Ndipo mkazi wachikulireyu apa, iye anadzinenera yekha kuti ndi Mpingo wa Mulungu; koma, chimene iye anali, iye anali atakongoletsedwa mu chuma ndi ngale, ndi chirichonse, ndipo anali nacho chikho cha zonyansa za ziwerewere zake, kuti iye anawapangitsa mafumu onse a dziko lapansi aledzere ndi vinyo wake. Nkulondola uko?

⁹⁸ Tsopano, ife tikumupeza iye apa kuti iye akutchedwa “Yezebeli.” Ndipo Yezebeli, choyipa chimene Yezebeli anachita, atangofika pakati pa Aisraeli amenewo, iye anawapha iwo ndipo anachita chirichonse chimene iye akanakhoza, ndipo—ndipo anamanga maguwa ake a nsembe. Nkulondola uko? Ndizo ndendende zimene mpingo wa Katolika unachita. Ndizo ndendende. Koma tsopano tiyeni tiwerenge mopitirira pang’ono. Izi zikudodometsani inu. Nthawizina iwe ukadodoma, umadya mowonjezera pang’ono.

. . . akudzitcha *yekha mneneri wamkazi*, (Tsopano, ngati iye akunena kuti, “Ndine wotanthauzira yekhayo wa Mawu.”) ndipo amaphunzitsa ndi *kunyenga akapolo anga kuti achite* ziwerewere, . . . *kudya zinthu zoperekedwa nsembe kwa mafano*.

⁹⁹ M’bale uja yemwe anafunsa za “serpenti,” za “kudya chipatso mmunda wa Edeni.” Inu mukuona zomwe izo ziri (Sichoncho inu?) pamene Iye anati, “kudya,” apa. Chimene icho chinali, chinali mwauzimu, inu mukuona. Ndipo a . . . ndipo . . .

Ndipo ndinampatsa iye danga kuti alape chifukwa cha chiwerewere chake—chiwerewere; ndipo iye sanalape.

Taonani. Ine ndidzamponya iye pa kama, . . . (Kama wa mtundu wanji? Wa chidziko. Ndizo ndendende zomwe iye ali lero.) . . . ndi iwo amene akuchita chigololo naye kulowa chisautso cha chikulu, kupatula iwo atalapa za ntchito zawo. (Uku ndikupita mpaka mu Chisautso Chachikulu.)

Ndipo . . . ndidzapha ana ake ndi imfa; . . .

¹⁰⁰ Whoa! Ndani ake? Mtsikana wakale uyu anali ndi ana ena. Tsopano Chivumbulutso 17. Ndi angati a inu . . . ? Nonse a inu munali pano usiku wathawu, ine ndikuganiza. Chabwino. Chivumbulutso 17, wachiwerewere wakale uyu, mpingo wa Katolika, unatchedwa “hule,” ndipo iye anali “manthu wa timahule.” Sakanakhoza kukhala anyamata, iyo inali *mipingo*.

¹⁰¹ Tsopano kodi mpingo wa Lutheran unachokera kuti, onsewa akuchokera kuti? Kodi bungwe lirilonse linachokera kuti? Chiyambi chake cha izo chiri pati, Laodikaya? Achinikolai potsiriza anapangidwa kukhala chimenecho; ndicho ndendende chinthu chomwecho kachiwiri. Inu simungathe kuzithandiza izo, m'bale. Oh, Eliya anafuula motsutsa chinthucho mu tsiku lake. Yohane anafuula motsutsa izo mu tsiku lake. Inde, bwana! Inu musaganize kuti munene mwa inu eni, "Ife tiri naye Abrahamu atate wathu: pakuti ine ndinena kuti Mulungu ndi wokhoza mwa miyala iyi kudzutsa ana kwa Abrahamu." Mukuona? Basi sangathe kuthandizidwa.

¹⁰² Tsopano, iye anali ndi ana. Kodi Yezebeli weniweni anali ndi ana? Inde, bwana! Mvetserani:

. . . Ine *ndidzapha ana ake* . . .

¹⁰³ Chiyani? Mpingo wa Katolika, ana ake ndi chipembedzo cha Chiprotestanti. Mwaona, ndizo ndendende, chifukwa iwo akuchita chinthu chomwe chomwecho. Anabatizidwa mwa iye mwa ubatizo wachirendo wawo, ubatizo osati wa mwamalemba; kugwirana chanza kuti alandire Mzimu Woyera; "Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera" mmalo mwa "Yesu Khristu." Ndipo kumachita chirichonse motsemphana ndi Baibulo. Komabe! Ndipo nkumayenda mpaka kulowa mmenemo.

¹⁰⁴ Mwana wake wamkazi ankatchedwa Athaliah, A-t-h-a-l-i-a-h. Iye anali naye iye. . . Iye, Yezebeli, anamukwatitsa Athaliah kwa Yehoram, mwana wa mfumu ya Yuda, ndipo posakhaltisa maguwa a Baala anali akuimirira mu Yerusalemu. Tsopano, inu simukusowa kuti mupite ku mbiriyakale ya izo, limenelo ndi Baibulo. Mukuona? Mwana wake wamkazi, Athaliah, anakwatiwa mwana wa mwamuna wa Yehosafati, yemwe anali Yehoram. Ndipo ana ake aakazi anachita chinthu chomwecho chimene iye anachita.

¹⁰⁵ Oh, mai! Kodi inu simukuziwona izo? Mwaona momwe mabungwe amenewa achitira, abale? Iwo anadzabwereranso kudzera mwa Luther ndi iwo, ndendende basi, ndipo anadzipanga okha bungwe pamodzi mmalo molola Mzimu Woyera. Ndipo Achipentekoste achita ndendende chinthu chomwecho. Iwo samawulola basi Mzimu Woyera kuti uzipita patsogolo ndi kukhala ndi mpata Wake, ndi kumapitirira; ndipo kuwala kulikonse kukabwera, ingokupimani iko ndi Mawu, ndi kumapitirira nazo. Iwo samawulola Mzimu Woyera kuti uzitsogolera, iwo anapanga bungwe ndipo anazidula kuchoka kwa china chirichonse chomwe chikanadzabwerapo. Anabwerera molunjika mmbuyo ndipo anadzikwatitsa mu chinthucho kachiwiri! Ndendende basi. Ife tikadzafika ku m'badwo umenewo, inu mungopenyerera zomwe zikukudikirirani inu mmusi panjirayi apa. Mukuona? Anadzakwatiwanso momwemo! Yesu ananena apa, "Iye. . .

Yezebeli uyu, iye amadzitcha yekha ‘mneneri wamkazi,’ ndipo Ine ndidzamuponyera iye pa kama wachidziko, ndipo ndidzapha ana ake” (Tsopano, mtundu wanji . . . ?) “ndi imfa.”

106 Kodi ndi chiyani . . . ndi imfa ya mtundu wanji yomwe ana ake amaphedwa nayo? Inu mukuona kuti iwo afa tsopano! Afa mwauzimu! Iwo alibe vumbulutso! Iwo amadziwa bungwe lawo, iwo amadziwa katekisimu wawo, iwo amadziwa chiphunzitso chawo cha mpingo; koma zikafika pakumudziwa Mulungu, ena a iwo sadziwa zochuluka za Iwo kuposa momwe Nkafula angadziwire za usiku waku Igupto; uko nkulondola, pamene zifika pakuwudziwa kwenikweni Mzimu Woyera. Ndikudabwa; kuwutcha Iwo . . . kufuna kuwutcha Mzimu wa Mulungu “wambwebwe,” kapena “mdierekezi,” za . . . pozindikira mizimu, ndi zinthu monga zimenezo, ndi kutulutsa adierekezi. “Bwanji, iye sali wa gulu lathu. Gulu limenero, oh, *bruu*.” Mwaona, basi iwo sakudziwa. Ndipo kenako nkulemba Ilo ndi—ndi dzina la “Yesu Yekha,” kapena mtundu wina wa “woyera-wodzigudubuza,” kapena—kapena mtundu wina wa chinthu chonga chimenecho. Sakudziwa basi!

107 Ndipo ora layandikira limene chinthu chimenecho chiti chidzayalutsidwe. Ndizo ndendende. Mulungu adzachita zimenezo motsimikiza basi monga ine ndaimira kuseri kwa guwa ili, chifukwa Iye adzawasasira ana Ake panja motsimikiza monga momwe ine ndaimira pomwe pano. Mulungu Kumwamba akudziwa zimenezo. Inu mukundikhulupirira ine kuti ndine mneneri wa Ambuye, wantchito wa Ambuye, inu mundimvere ine. Iye ali pafupi kwambiri. Inde, bwana.

108 “Ana ake adzaphedwa ndi imfa yauzimu.” Tayang’anani pa iwo: ozizira ndi ofunda. Tayang’anani pa . . . tayang’anani pa athu . . . Ife sitikusowa kuti tiyankhule za Abaptisti ndi Apresbateria, ife tikudziwa kuti iwo akhala akufa kwa zaka. Chiyani . . .

109 Pamene Luther anali ndi chitsitsimutso chake, kulungamitsidwa, ngati iye akanati . . . Ngati iye akanapitirirabe, izi—izi kusuntha kwakukulu kwa Chipentekoste uku tsopano kukanakhala mpingo wa Chilutera. Kuwala kukanabwera mwa kuyeretsedwa, Wesley akanamutsatira. Iye . . . Luther sakanatsatira zimenezo. Ayi, bwana, iwo anali kale Achilutera.

110 Chotero kenako Wesley anadzabwera. Wesley atafa, ndiye chinachitika ndi chiyani? Iwo anapanga bungwe zimenezo, ndipo anapanga Chimethodisti cha Wesley, Primitive Wes- . . . oh, mitundu yonse ya Amethodisti. Mukuona? Ndipo pamene . . . Anali ndi chitsitsimutso chachikulu, koma pamene iwo anadzaponyeramo bungwe, chinachitika ndi chiyani pamene Apentekoste anadzabwerapo ndikuyankhula mmalirime ndi

kubweretsapo kubwezeretsa kwa mphatso? Iwo sanathe kusuntha; anawatcha iwo ziwanda.

111 Tsopano kodi Apentekoste achita chiyani? Chinthu chomwecho chimene iwo anachita! Ndipo kodi iwo ali kuti? Akufa basi monga msomali wa pachitseko. Inde, bwana! Ndizo ndendende. “Ine ndidzaponyera ana ake pa kama wa—pa kama wa imfa, ndi kuwapha iwo.” Chabwino, ndiroleni—ndiroleni ine ndiwerenge zimenezo kuti inu muone apa, ine ndikukhulupirira iyo inali ndime ya 22:

Ndipo *ine ndidzamponya iye pa kama, ndi iwo amene akuchita chigololo naye* kupita ku *chisautso chachikulu*, (chi—Chisautso Chachikulu) . . .

112 Ndi zomwe zikuchitika. Tsopano kumbukirani, ndiroleni ine ndiime apa miniti yokha, Chisautso Chachikulu chija ndi chimene—chimene chidzaponyere mmenemo, anthu amenewo omwe ndi anamwali opusa omwe analibe mafuta mu nyali zawo; komabe iwo anali a bungwe, anthu abwino, ankapita ku tchalitchi, chirichonse; koma iwo anadzera kudzapeza mafuta, koma mochedwa kwambiri pamenepo. Mwaona, adzamuponya iye mu Chisautso Chachikulu, iye adzakalowa mmenemo, mpingo wa Katolika udzakalowamo, ana ake onse adzakalowa naye limodzi, mu Chisautso Chachikulu.

. . . *pokhapokha iwo atalapa za zochita zawo.*

113 Osati—osati ana omwe ali mmenemo; koma mpingowo pawokha, amenewo ndi ana ake (ndi bungwelo), osati anthu omwe ali mmenemo, monga Akatolika osauka, Abaptisti, Apresbateria, kapena Apentekoste. Ine ndimawamvera iwo chisoni. Basi, “Chabwino, ine . . .”

“Kodi ndinu Mkhristu?”

“Chabwino, ndine wa Presbateria.” Oh!

114 Izo ziribe kanthu kochita nkomwe ndi Izo kuposa kunena kuti “nkhumba yokhala ndi chishalo chammbali inali akavalo ampikisano.” Chotero mungachite nazo chiyani zimenezo mdziko? Bwanji, palibe nkomwe. Ine sindinatanthauze zimenezo mwanthabwala, ndizo . . . izi sikuti . . . si malo a nthabwala, uwu ndi—uwu ndi Uthenga. Mukuona? Ine ndimangofuna kuti ndipereke chitsanzo. Mwaona, koma izo—uko nkulondola. Mwaona, iwo alibe konse—alibe chochita nawo Iwo kuposa kalikonse.

“Ndine wa Pentekoste.”

115 Zimenezo ziribe kanthu kena kochita ndi Iwo kuposa kalikonse. Iwe ukhoza kukhala wa mabungwe awo forte-leveni, koma kodi ndiwe mwana wobadwa mwatsopano wa Mulungu? Kwenikweni, kodi iwe umamukonda aliyense ndi mtima wako wonse, ndi solo yako, ndipo kodi umamukonda Mulungu, ndipo umakhala tsiku ndi tsiku . . . ziribe kanthu zomwe aliyense

angakuchitire iwe? Ngati iwe ukufufuma ndi kunena kuti, “Humm!” ngati macheke, izo zimangowonetsera kuti Mzimu Woyera wachokapo, ngati unayamba wakhalapo nawo Iwo.

116 Taonani:

. . . pokhapokha iye *alape za zintchito* zimenezo.

Ndipo Ine ndidzapha ana ake ndi imfa; . . .

117 “Ana ake,” a Yezebeli. Tsopano, Yezebeli anachita chiyani? Anamkwatitsa mwana wake wamkazi mu udindo wina (wa Yuda) kumeneko, uko mu Yuda. Tsopano penyani kugwirizana kwake kwauzimu. Mwinamwake ine ndikhoza kuzijambula izo. Apa, penyani izi mwatcheru kwenikweni tsopano:

118 *Apa* pali Yezebeli, ndi Israeli. Koma *apa* pali Yuda, mtundu wosiyana cha kuno, kwa winawo; uwu ndi wa Yehosafati *kuno*. Chabwino. Tsopano, uyu apa anali Ahabu; tsopano apa pali Yezebeli mkati *munu*. Tsopano, iye akubwera *kuno* ndipo akudzachititsa Israeli yense kupita ku kupembedza mafano.

119 Ndizo ndendende zomwe mpingo wa Katolika unachita mmbuyo mu masiku ake pamene Konstantini anawagwirizanitsa Achinikolai (machitidwe ozizira kumtunda *kuno*) kulowa ku—ku—mu mpingo ndi ku chikunja, ndipo anapanga kachitidwe kachikunja ka Chikhristu. Ine sindikufuna kuti ndipweteke kumverera kwanu, anthu Achikatolika, koma ine ndikayankhira pamaso pa Mulungu. Ndizo zonse zomwe mpingo wa Katolika uli, ndi mawonekedwe achikunja a Chikhristu: tizikhulupiriro, ndi mafano, ndi china chirichonse. Ndiko kulondola ndendende, mawonekedwe achikunja basi. Tsopano, izo nzoona. Ngati ine ndikufa mu miniti ino, ndicho choonadi. Ndipo Achiprotestanti ali momwemo mu chinthu chomwecho, kungoti mu gulu lina.

120 Tsopano penyani chimene Yezebeli anachita. Ndiye, inu muwona, m—mdierekezi. . . Iye anali wodzipereka kwambiri, iye anawatenga ana ake aakazi. Iye anali ndi mwana wamkazi amene anabadwa *kuno*, ndipo mwana wamkazi uyu akupita cha *kuno* kwa muntu wotchuka woyera uyu ndipo akumutenga ndi kukwatiwa mwana wake wamwamuna; ndipo akubweretsa chinthu chomwe chomwecho *kuno* kuchokera kwa Yehosafati, kupita ku mbali ino.

121 Tsopano, Achinikolai enieni, Achinikolai, machitidwe ofunda omwe amafuna bungwe limenero, iwo anakwatiwa mwa ilo *kuno*. Ndipo tsopano zindikirani chinthu chomwecho. Iwo anamutengera Yezebeli *kuno* (mpingo wa Katolika), ndipo kumusi *kuno* iye akumutenga mwana wake wamkazi (mabungwe ake) ndi kukamkwatitsa iye kwa iwo kumusi uko, ndipo akuchita chinthu chomwecho kwa iwo. “Ndidzapha ana ake ndi imfa,” imfa yauzimu. Kudzipangira okha bungwe ku imfa, ndipo chinthu choyambirira inu mukudziwa, Mzimu wonse wapita.

122 Ndiuzeni ine. Ndiroleni ine ndingokufunsani inu chinthu chimodzi, wazambiriyakale aliyense pano, zomwe ine ndikudziwa mulipo faiwi kapena sikisi a inu mwakhala pano. Ine ndikufuna inu mubwere mudzandiwonetse ine Lemba limodzi kapena—kapena mutu umodzi wa—wa mbiriyakale, pamene uliwonse wa mipingo imeneyo inagwapo ndi kubwerera mu bungwe imene inadzawukanso ndi chitsitsimutso. Ndiuzeni ine. Pamene iwo anadzipanga okha kukhala bungwe, kodi anayamba akhalapo nacho chitsitsimutso iwo atatha kupanga bungwe? Ayi, bwana! Mzimu umawasiya iwo. Ine ndikuphatikizapo Apentekoste.

123 Pamene Madalitso Apentekoste anagwa, ndipo inu nonse munayankhula mmalirime, inu a nthawi zakale, mutakhala nawo Madalitso aakulu Achipentekoste awo ndi zinthu, munagwa. Patapita kanthawi inu munakhala ndi zomwe inu munazitcha General Council. Mgwirizano ndi wabwino, koma osati bungwe. Chinthu choyamba inu mukudziwa, iwe sungakhoze kupirira zimenezo, iwe umayenera kubwerera mmbuyo ndi kukakhala “mwana wa . . . Satana,” ndikudzipanga wekha bungwe.

124 Ndiyeno Kuwala kwina kunadza, kwa Dzina la Yesu Khristu. Kenako iwo onse anakanika, ndipo anati, “Mulungu adalitsike, ngati inu mulibe dzina la Yesu, inu mukupita ku gehena. Ndipo ife tiri nalo Ilo, ndipo inu mulibe Ilo.” Kodi iwo anachita chiyani? Anangofera pomwepo ali panjira yawo; anapanga bungwe kuchokera mu zimenezo. Mukuona? Mmalolo molola kuti Kuwala kungoyenderera kudutsa mu mpingo, izo basi pazokha zikanatenga malo ake. Koma inu mumadzipanga nokha bungwe. Ndi chiyani chimenecho? Mwana wa Yezebeli. Ndipo iwo onse anafa, limodzi.

125 Tsopano ine ndikufuna ndikufunzeni inu chinachake. Kodi a Assemblies of God, kapena a Oneness, kapena—kapena aliyense wa iwo anadzukapo mu chitsitsimutso chachikulu chogwirizana? Ayi nkomwe! Chitsitsimutso chapitachi changowadutsa pomwepo, chimene Mzimu Woyera unatsika pa mtsinje (ambiri a inu mwakhala pano pakali pano) mu 1933, ndipo msonkhano waukulu uwu wa machiritso umayenera kuchitika, anati, “Icho chidzasesa dziko lonse,” ndipo icho sichinabwere konse kudzera mu bungwe lina lirilonse nkomwe. Mulungu anapita kunja kwa mikombero ndipo anakadzutsako wachikunja, pafupifupi, kuti ayambe chitsitsimutso chimenecho. Ndipo taonani chimene Icho chachita! Mukuona?

126 Mabungwe amenewo, mwamsanga iwo akangochita bungwe, iwo amafa. Iye anati, “Ine ndidzapha ana ake ndi imfa.” Oh, mai! ine ndikudziwa inu . . . Chonde musaipidwe nane ine, koma ine . . . Ngati ine ndikuzidziwa Izi ndipo osazinena Izo, ndine wachinyengo wotsikitsitsa, ndipo Mulungu adzandiyimba

ine mlandu chifukwa cha Izo. Ine ndikufuna kukhala monga Paulo, “Osaleka kulengeza uphungu wonse wa Mulungu.” Uko nkulondola. Chabwino. Chabwino.

¹²⁷ Tsopano, ndipo iwo anamanga maguwa mu Yerusalemu. Tsopano ine ndikufuna kuti ndiwone. . . Ndipo pamene Yezebeli anadzakwatiwa ndi Ahabu, iye anabweretsa mafano kuti Israeli adziwagwadira. Chinateronso chiphunzitso cha Chinikolai, chinakwatirana ndi chikunja; anagwetsera pansi Jupiter, anakamuikapo Petro; ndi Venus, kwa Maria; ndipo monga Baibulo linanena, “Iye anapangitsa Israeli yense kuchimwa.”

¹²⁸ Momwemonso mpingo wa Katolika wapangitsa ana onse aakazi kukwatiwa ndi bungwe, ndipo chinthu chonsecho ndi tchimo, monga Yezebeli kwa mwana wake wamkazi. Chabwino. Ndipo pochita izi pamene ulamuliro unakhazikitsidwa, ndipo Papa Boniface—Boniface III nkudzatenga mpando wake, ndipo iwo anali ndi—ndi mulungu pampando wachifumu, iwo analibenso nawo ntchito ubatizo wa Mzimu Woyera mu mpingo. Uko nkulondola. Iwo anatenga tizikhulupiriro tawo ndi miyambo, ndi kumapitirira.

¹²⁹ Ndipo pamene bungwe linadzavomereza chiphunzitso chomwecho, iwo anapondereza ufulu wa Mzimu Woyera mu mpingo, Baptisti, Presbateria, Methodisti, ndi ena otero. Iwo ndithudi anatero! Ndipo pang'onopang'ono ife tikuwawona iwo akufota ndipo akufa monga Yesu ananena za mpesa. Tsopano, Mzimu Woyera wonse mu zizindikiro ndi zodabwitsa unakaikidwa mmbuyo mu tsiku lapitalo. Ndipo iwo alemera, monga iye anachitira. Chotero iye anachititsa dziko lonse kuti lichimwe, chifukwa iye wapita ku fuko lirilonse, iye ndi ana ake aakazi. Ndiko kulondola.

¹³⁰ Tsopano tamuonani Iye akumuitana iye mu m'badwo wa mpingo wina tsopano. Muwoneni Iye akumuitana iye. Muwoneni Iye akuchonderera mmusi kumapeto kuno, ndipo akutulutsako Wotsalira Wake, “chifukwa cha Osankhidwa,” apang'ono chabe, kuti palibe mnofu womwe ukanadzapululumutsidwa ngati. . . enawo ayi.

¹³¹ Monga kwalembedwa mu Chivumbulutso 13: 6. Inu mukufuna kufika kwa izo mphindi imodzi yokha? Kuti Iye anati Iye. . .kuti “Mkazi uyu anapangitsa onse kulandira chilemba (chirombo ichi chinatero), anapangitsa onse kuti alandire chilemba (onse osauka, aakulu, aliynse yemwe iwo anali), chilemba cha chirombo,” amene anali Mpingo wa Roma Katolika.

¹³² Mwina zimenezo kapena iwo anapanga fano. . . Chivumbulutso 13:14, iwo anapanga fano kwa chirombo. Inu—inu. . .Ine ndikuganiza inu nonse mukuwerenga zimenezo. Ngati inu simunatero, bwanji, ife titembenukira mmbuyo ndipo tiwerenga izo. Chivumbulutso 13:14:

Ndipo iye ananyenga iwo akukhala pa dziko lapansi mwanjira ya zozizwitsa zimenezo chimene iye anali nayo mphamvu yakuchichita pamaso pa chirombo; (Ndicho chitaganya ichi cha mpingo)...ndi kuchita pamaso pa chirombo; kunena kwa iwo akukhala padziko lapansi, kuti iwo apange fano kwa chirombo, chomwe chinali ndi bala lakufa nalo (chikunja)... ndipo anali ndi lupanga, ndipo anakhala moyo... (kudzera mu upapa, Roma wachikunja mpaka Roma waupapa. Mukuona?)

133 “Anapanga fano kwa iye.” Kodi izo zingakhale chiyani? Basi zomwe iwo akuchita pakali pano, ndendende basi, akusunthira mmwamba mu chitaganya cha mipingo ichi, “Mipingo yonse ili mu bungwe ili, yonse yapita mu gulu limodzi.” Tsopano iwo akutenga Baibulo. Ndipo Papa Yohane wawaitanira iwo onse kuti abwerere. Bishopu wamkulu waku Canterbury, onse akupita kumeneko. Chinthu choyambirira inu mukudziwa, chinthu chonsecho chikubwerera kumene kwa *Manthu*, chifukwa iwo ndi achiwerewere kuyamba ndi kuyamba. Mukuona? Iwo amati, “Ife tonse tigwirizana limodzi pa cholinga chimodzi chachikulu cholimbana ndi Chikominisi.” Ndipo sakudziwa kuti Mulungu anadzutsa Chikominisi (ine ndikhoza kutsimikizira izo ndi Baibulo ili.) ndipo mpaka anaika mmaganizo mwawo za iwo kuti awabwezerere oyera, magazi omwe iwo anakhetsa padziko lapansi. Mulungu anakhazikitsa Chikominisi chimodzimidzi monga momwe Iye anamupangira Mfumu Nebukadinezara kuti—kuti alange Israeli. Iye anadzutsa chikominisi, ndipo tsiku lina iye adzamuphulitsa Roma kumuchotsa pa mapu. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. Ndizo ndendende. Mulungu anena chomwecho. Uko nkulondola.

Ine ndimatsutsana ndi chikominisi; icho chimatsutsana ndi Mulungu. Ndithudi izo ndi choncho. Koma inu musamakhale ndi chidwi kwambiri ndi Katani la Chitsulo ilo, koma muzisamalitsa katani la pepo lija. Mukawerenge Foxe’s *Book of Martyrs* ndipo inu mukaziwona izi, uko nkulondola.

134 Tsopano tiyeni tiwone kumene ife... Ndiyeno inu muwona apa tsopano kuti iye anapangitsa onse (olemera, osauka) kulandira chilemba; koma pali gulu limodzi limene iye sangathe kuligwira. Inu mukudziwa zimenezo? Chivumbulutso 13: . . . 8.

135 Mvetserani izi. Ndiloreni ine ndiwerenge izi:

Ndipo ine ndinaimirira pamchenga wa mnyanja, ndipo ndinawona chirombo chikutulukira kuchokera mnyanja, chokhala nayo mitu seveni ndi nyanga teni, . . . pa nyanga. . . akorona, ndi pa mitu dzina la mwano. (Ndiwo mapiri seveni; ife tinazitenga zonsezo usiku wathawu, inu mukudziwa.)

Ndipo chirombo chimene iwe unachiwona chinafanana ndi nyalugwe, . . .mapazi ngati—ngati chimbalangondo, ndi pakamwa pake. . .pakamwa pa mkango: ndipo chinjoka (Chimene chinali mdierekezi wofiira amene anayima pamaso pa mkazi kuti amulikhwire mwana wake, yemwe anali Roma, ife tonse tikudziwa.) . . .ndipo anampatsa iye. . .mphamvu, ndi mpando wake, ndi ulamuliro wawukulu.

Ndipo ine ndinawona umodzi wa mitu yake ngati unali wovulazidwa mpaka kuimfa; (chikunja, mwaona) . . .ndipo bala lake lakuimfa linachiritsidwa: (upapa ukutenga malo ake, unalumikizana ndi Chikhristu, ndi Chinikolai) . . .ndipo dziko lonse linazizwa potsatira chirombocho.

136 Chikatolika chasesa kupita mu fuko lirilonse pansi pa miyamba. Uko nkulondola. Monga ananenera Daniele za chitsulo kulowa mu dongo, ndi zina zotero.

137 Ndipo ine ndikupatsani inu kanthu kakang’ono pa izo, icho ndi “chitsulo ndi dongo.” Kodi inu munazindikira, kapena kodi ine ndinayamba ndabwerezapo izo kwa inu, pa msonkhano waukulu womaliza uja umene iwo anali nawo kumtunda kuno kumene Khrushchev anavula nsapato yake ndi kumenyetsa nayo tebulo? Pamenepo panali mafuko faivi akummawa omwe anasonkhana kumeneko, panali mafuko faivi akumadzulo. Khrushchev ankatsogolera mafuko akummawa, Eisenhower anatsogolera mafuko akumadzulo; pamenepo panali atsogoleri awiri aakulu, zala zazikulu ziwiri zakumapazi. *Khrushchev*, ku Russia, amatanthauza “dongo.” *Eisenhower*, mu Amer. . . mu Chingerezi, zimatanthauza “chitsulo.” Ife tiri kumapeto.

Ndipo iwo anachipembedza chinjokacho, chimene chinapereka mphamvu kwa chirombocho: ndipo. . . (Umenewu ndi uthenga wathu wotsatira pano pa kachisi, inu mukumvetsa.) . . .ndipo iwo anachipembedza chirombo, akuti, Ndani angafanane ndi chirombocho? ndipo akhoza ndani kuchita nkondo ndi iye?

138 Mwa kulankhula kwina, taonani apa. Eisenhower ali—ali ndi dzina lalikulu kuno mu United States uyu, koma ku Roma iye si kanthu; Russia, iye si kanthu. Khrushchev ndi wamkulu ku Russia, koma ku United States iye si kanthu. Koma pali munthu mmodzi yemwe ndi wamkulu konsekonse, ndiye papa ameneyo (Uko nkulondola.) “Tiyeni tidzipange tokha bungwe limodzi, ndipo tibwere pamodzi.”

Ndipo pamenepo kunapatsidwa kwa iye kamwa kuti ayankhule zinthu zazikulu. . .mwano; . . .mphamvu inaperekedwa kwa iye kuti apitirize miyezi forte thuu.

Ndipo iye anatsegula kamwa yake, ndipo anachitira mwano Mulungu, (ndi “kuphunzitsa chiphunzitso malamulo a anthu; ammutu, amalingaliro apamwamba, okonda zosangalatsa; okhala nawo mawonekedwe aumulungu, nkumakana Mphamvu yakeyo”) . . . ndipo anachitira mwano dzina lake, (Anatenga “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera” mmalo mwa “Ambuye Yesu Khristu.” Mukuona?) ndi kachisi wake, ndi iwo akukhala mkati . . . ku—kumwamba.

Ndipo kunapatsidwa kwa iye kuchita nkondo ndi oyeru, (pamenepo pakubwera chisautso) ndi kuwagonjetsa iwo: ndipo mphamvu inaperekedwa kwa iye pa mitundu yonse, . . . zinenero, ndi mafuko.

Ndi iwo onse okhala padziko lapansi—dziko lapansi adzamupembedza iye, omwe maina awo sanalembedwe mu bukhu la moyo wa Mwanawankhosa wophedwa kuchokera ku maziko a dziko lapansi. (Oh, oh, oh, oh, oh, oh, oh.)

139 “Maziko adziko lapansi.” Maina athu, ngati iwo anakhalapo pa Bukhu, analembedwa kumbuyo kumeneko. Yesu anati, “Palibe munthu angadze kwa Ine kupatula Atate Anga atamukoka iye poyamba, ndipo onse amene Atate andipatsa Ine adzadzwa kwa Ine. Nkhosa Zanga zimamva Liwu Langa,” (Ichi ndi Chakudya, mwaona.) “ndipo mlendo . . .”

140 Ndiye iye akhoza kunena kuti, “Chabwino, ine ndinangojowina tchalitchi, ndine wabwinonso ngati inu.” Chimenecho si Chakudya cha nkhosa.

141 Pano pali Chakudya cha nkhosa, “Kukhala limodzi mmalo Ammwambamwamba mwa Khristu.” Oh, Iye ndi wodabwitsa kwambiri! Sichoncho Iye? Chabwino.

142 Tsopano tiyeni titsirize mofulumira kwambiri chifukwa ndi, eya, nthawi yadutsa tsopano. Chabwino. “Koma ine ndikuti . . .” Tiyeni tiwone tsopano, ine ndiri nayo ndime ya 23:

Ndipo Ine ndidzawapha ana ake ndi imfa; ndipo mipingo yonse idzadziwa kuti Ine ndine Iye amene ndimafufuza impsyo ndi mitima: ndipo ine ndidzapereka kwa aliyense wa inu molingana ndi ntchito zanu.

Koma ndinena kwa inu, ndi kwa ena onse mu Tiyatira, onse amene alibe chiphunzitso ichi, . . . (Chinali chiphunzitso cha mtundu wanji chimenecho? Bungwe, mabishopu, ndi ma archbishopu, ndi mapapa, mwaona.)

143 “Alibe chiphunzitso ichi.” Tsopano, Baibulo, ife tinapeza usiku watha kuti Israeli, akubwera kudutsa Moabu, iwo sanali fuko. Iwo ankakhala pa nkhope ya dziko lapansi, ndipo iwo anali anthu, amfulu. Nkulondola uko? Choimira; oyendayenda,

mahahema ndi zina zotero. Magulu achipentekoste ali mwanjira yomweyo, achipentekoste owona, akuyendayenda malo ndi malo. Mukuona? Chabwino.

. . . ndipo alibe *ayi chiphunzitso ichi* (koma adzipanga okha bungwe, ndipo akupanga bungwe lalikulu kuchokera mmenemo) . . . zomwe *ziribe izi* . . . ndipo *amene sanadziwe kuya kwa Satana*, . . .

144 Tsopano kumbukirani ife tinapeza kumene mpando wa Satana unali. Usiku wapitawu tinamutenga iye kubwerera mpaka ku chiyambi. Kodi mpando wake unali kuti pachiyambi? Babeloni. Ndipo Babeloni. . . Pamene u—ulamuliro, mfumu-wansembe waku Babeloni, anali kuthamangitsidwa ndi Akasidi ogonjetsa, iye anabwera ku Pergamo ndipo anadzapangako mpando wake. Mwaona, anasuntha mpando wake kuchokera ku dziko la Sina kupita ku Pergamo. Ife tangowerenga kumene izo mu mbiriyakale usiku wathawu. Ndipo tsopano apo iye anayambira pamenepo, anapanga mpingo wa Katolika, womwe mpaka pano ukadali mayi Babeloni. Chabwino, “Mpando wa Satana.”

. . . ndi mpando *wa Satana, monga iwo amalankhulira; Ine sindidzaika zolemetsa zina pa inu.*

145 “Sipadzakhalanso zolemetsa zina; basi zomwe inu muli nazo kale.” Ochepa aang’ono awa omwe ali mmenemo, mwaona, onse amene afinyidwira kunja mu M’badwo wa Mdima uwu. Tsopano ndi pafupifupi zaka fifitini handiredi iwo anadutsa zimenezo.

Koma icho chimene muli nacho kale gwiritsitsani kufikira Ine ndidzabwere. (Mwakuyankhula kwina, “Inu muli ndi Madalitso Achipentekoste akadali mmitima yanu. Gwiritsitsani zimenezo mpaka Ine ndidzabwere kuti ndidzakupatseni inu mpumulo, pakuti m’badwo wotsatira uwu ukungobwera mu nthawi yotsatira.”)

. . . *iye amene alakika, ndi kusunga mawu anga kufikira chimaliziro, kwa iye Ine ndidzampatsa ulamuliro pa mafuko:*

Ndipo iye adzawalamulira iwo ndi ndodo ya chitsulo; ndipo monga mbiya ya wowumba iwo adzaphwanyidwa mu kunjenjemera: ngakhale monga Ine ndalandira kwa Atate anga.

146 Inu mwaona, Mpingo umenewo, zidzakhala bwanji pamene Mpingo wa M’badwo wa Mdima uwo udzawuka kuti uyime pa chiweruzo motsutsana ndi gulu lachikunja lija la. . . kumbuyo uko? Kodi iwo adzaponderedwa pansu! Mapazi amenewo amkuwa adzaponda pomwepo, ine ndikukuuzani inu! “Iye adzawaphwanyanya iwo kukhala zidutsa,” Baibulo limatero.

*Ndipo Ine ndidzapereka kwa iye nyenyezi ya mmawa.
(Inu mukudziwa chimene iyo ili, sichoncho inu? Khristu
ndiye “Nyenyezi ya Mmawa.” Chabwino.)*

*Iye amene ali ndi khutu, muloleni iye amve chimene
Mzimu ukunena kwa mipingo.*

147 Oh, mai! Kodi inu sindinu okondwa! Tachedwa pang'ono. Ine ndiri ndi zina, ine ndidzazitenga izo mwinamwake mawa usiku, pa izi za zaka thuu sauzande pamenepo.

Koma Iye ndi Kakombo wa Mchigwa, Nyenyezi
Yowala ndi ya Mmawa,
Iye ndiye wokongola kwambiri mwa zikwi
khumi ku moyo wanga.
Kakombo wa mchigwa, mwa Iye yekha
ndikumuwona,
Zonse zomwe ndikufuna...ndi kundipanga
ine kukhala wamphumphu.
Mu chisoni Iye ndi mtonthozi wanga,
mmasautso Iye ndi pokhalapo panga,
Iye amandiuza chisamaliro chonse pa Iye
ndikankhire.
Aleluya!
Iye ndi Kakombo wa Mchigwa, Nyenyezi
Yowala ya Mmawa,
Iye ndiye wokongola kwambiri mwa zikwi
khumi ku moyo wanga.

148 Kodi mukunkonda Iye? Oh, ine basi:

Ine ndinkonda Iye, ine . . .

Tsopano tiyeni timpembedze Iye tsopano, Mawu onse odula amenewo ndi Uthenga.

Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
Nandigulira chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

149 Kodi Iye si wodabwitsa! Ine ndinkonda Iye. Tsopano, zinthu zomwe ine ndaziphonya kuzifikira, zidzakhala mmabuku, za chidziwikireni, chifukwa ife sitingabweretse m'badwo wa mpingo wonse mu usiku umodzi. Ine ndinakhala ngati ndazitonholetsa izo pang'ono usikuuno, pa chifukwa chokhala wosasa mawu pang'ono. Koma, oh, kodi Iye si wodabwitsa! Oh! Hmm!

Kuli anthu pafupifupi kulikonse,
Omwe mitima yawo yonse ikuyaka,
Ndi Moto umene unagwa pa Pentekoste,
Umene unawatsuka ndi kuwapanga iwo
kuyera;
Oh, Mukutentha tsopano mkati mwa mtima
wanga,

Oh, ulemelero kwa Dzina Lake!
 Ndine wokondwa kunena kuti ndine mmodzi
 wawo.

Oh, mmodzi wawo, ndine mmodzi wawo,
 Ndine wokondwa kunena kuti ndine mmodzi
 wawo, (Aleluya!)
 Mmodzi wawo, mmodzi wawo,
 Ndine wokondwa kunena kuti ndine mmodzi
 wawo.

¹⁵⁰ Kodi ndinu okondwa? Ine ndikukumbukira ndikubwera kuchokera ku Chattanooga usiku wina; ndipo ndege inatsitsidwa ku—ku—ku Tennessee, kumusi uko ku Memphis. Iwo anandiika ine mu hotelo yayikulu imeneyo, yabwino kumeneko. Ndipo anandiitana ine, anati, “Ndege itulukira ikamakwana—ikamakwana seveni koloko, mmawa mwake.”

¹⁵¹ Ndipo ine ndimatenga makalata ena kuti ndikawayike mu bokosi la makalata; obwera kunyumba, ndimawaleMBERANSO azimzanga ena. Ndipo ndikutsikira kumeneko, Mzimu Woyera unati, “Kazipitirabe kumayenda.” Ine ndinali ndikumapitirabe, ndinakafika ku mzinda wa achikuda.

¹⁵² Ine ndinali nditaima pansu apo, ine ndinaganiza, “Mai! Onani apa, yakwana nthawi yoti ndege ija izipita.”

¹⁵³ Ndipo Mzimu Woyera unali ukunenabe, “Kazipitirira kumayenda.” Basi monga momwe Iye anachitira mu nkhalango tsiku lina kumusi uko, inu mukudziwa. “Kazipitirabe kumayenda.” Chotero ine ndinapitirabe kumayenda.

¹⁵⁴ Ine ndinapezeka kuti ndinayang’ana pansu kumusi uko, mu imodzi ya nyumba zazing’ono za achikuda izo kumene anthu achikuda anali kukhala, osauka, kumusi uko. Azakhali Jemima achikulire, kwenikweni, atavala malaya achimuna pamutu pake, atatsamira pamenepo. . . monga choncho.

¹⁵⁵ Ndipo ine ndinali ndikupita kumeneko ndikuyimba:

Ndine. . . wa iwo, ndine mmodzi wawo,
 Ndine wokondwa kunena kuti ndine mmodzi
 wawo, (Oh, Aleluya!)

“Ndipo Inu mukufuna chiyani, Ambuye?”

Mmodzi wawo, ndine mmodzi wawo,

Kodi inu mumakhulupirira mu kutsogozedwa ndi Mzimu?
 Inde, zedi.

Ndine wokondwa kunena kuti ndine mmodzi
 wawo.

¹⁵⁶ Zakhala ziri pafupifupi zaka fortini zapitazo tsopano. Iye anali akuyang’ana pa mpanda. Ine ndinali pafupifupi, oh, theka la mdadada wa mu mzinda kuti ndifike kwa iye, ndipo ndinamuwona dona wokalamba uyu, wachikuda

akundiyang'anira ine panshi, inu mukudziwa. Chabwino, ine ndimapitirirabe, ndinasiya kuyimba, ndinayamba kuyenda chotsika. Ine ndinaimirira pafupi ndi iye, misozi yayikulu kwambiri pa masaya aakulu onenepa amenewo; iye anayang'ana pa ine, anati, "Mmawa wabwino, Abusa!"

¹⁵⁷ Ndinapotoloka, ine ndinati, "Muli bwanji, Azakhali?" Ndipo iye anati. . . Ine ndinatembenuka, iye anali kuseka, anali ndi kumwetulira kwakukulu pankhope yake. Ine ndinati, "Inu munadziwa bwanji kuti ndine m'busa?" Kummwera kumeneko, inu mukudziwa, *mlaliki* ndi "m'busa." Anati. . . Ine ndinati, "Inu munadziwa bwanji kuti ine ndinali m'busa?"

Iye anati, "Ine ndimadziwa kuti inu mukubwera!"

Ndipo ine ndinati, "Inu munadziwa bwanji zimenezo? Inu mumandidziwa ine?"

Iye anati, "Ayi, bwana." Ndipo iye anati, "Ine ndimadziwa kuti inu mukubwera." Anati, "Kodi inu munayamba mwamvapo nkhani yokhudza mzimayi wa Chisunemu?"

Ine ndinati, "Inde, bwana."

¹⁵⁸ Ndipo iye anati, "Chabwino," iye anati, "Ine ndi mkazi wa mtundu umenewo." Iye anati, "Ndipo Ambuye anandipatsa ine mwana, ndipo ine ndinamuuza iye. . . ndinamuuza Iye kuti ine ndimulera iye." Anati, "Ndine mkazi wosauka. Ine ndimachapa ndikugwirira ntchito anthu achizungu kuti ndizipeza chithandizo." Iye anati, "Ndipo Iye anandiuza ine kuti Iye—Iye andipatsa ine mwana, ndipo ine ndinamuuza Iye kuti ine ndimulera iye." Anati, "Ine ndinamulera iye mwabwino momwe ine ndimadziwira kutero, koma" anati, "Abusa, iye analowa mu gulu lolakwika. Iye anatenga matenda, ndipo ife sitimadziwa kalikonse zokhudza izo." Anati, "Iye anafika nawo povuta. Ndipo iye akufa, ali umo pa bedi." Anati, "Iye wakhala ali chikomokere tsopano, masiku awiri." Anati, "Adokotala anabwera ndipo anati, 'Izo zadya mtima wake ndi zina zotero, inalowa mu magazi ake, moyipa kwambiri mpaka iyo yamuwononga iye; kotero kuti zinthu zomwe iwo amupatsa iye sizikumuthandiza iye tsopano.'" Ndipo anati, "Iye akufa." Ndipo anati, "Ine basi ndikulephera kuti ndipirire kuti ndimuwone iye akufa, wochimwa." Ndipo anati, "Ine ndinapemphera ndipo ndinapemphera," anati, "utali wa usiku wonse ine ndimapemphera." Anati, "Iye ali chikomokere, iye sakudziwa kalikonse." Anati, "Iye wakhala asali choncho kwa masiku awiri."

¹⁵⁹ Anati, "Ine ndinapemphera, ine ndinati, 'Ambuye, Inu mwandipatsa ine mwana ameneyo' ndipo anati, 'monga Inu munachitira mzimayi wa Chisunemu.' Anati, 'Ali kuti Eliya Wanu? Ali kuti. . .?' Anati, 'Chabwino, kuti—chiri kuti chinachake choti chindithandize ine?'"

¹⁶⁰ Ndipo anati, “Ine ndinagona pa maondo anga.” Ndipo iye anati, “Ambuye anayankhula nane, mmaloto anga,” ndipo iye anati, “‘Tuluka ndipo ukayime pachipata. Ndipo pakhala pakubwera munthu chotsika msewu, atavala chipewa chaching’ono, chotuwa ndi suti yoderapo.’ Iye anati, ‘Iye adzayankhula nawe.’”

¹⁶¹ Ndipo iye anati, “Ine ndakhala nditaima pano kusanache.” Ndipo ku nsana kwake kunali kutanyowa ndi mame. Ndipo iye anati, “Ndipo ine ndinakuwonani inu mukubwera mu chipewa chotuwa chimenecho,” iye anati, “koma inu mumayenera kuti mukhale mutanyamula kachikwama kakang’ono.”

¹⁶² Ine ndinati, “Ine ndachisiya icho mu hotelo.” Mukuona? Ndipo ine ndinati, “Mnyamata wanu akudwala?”

Anati, “Iye akufa.”

Ine ndinati, “Dzina langa ndine Branham.” Ine ndinati, “Kodi inu mukundidziwa ine?”

Iye anati, “Ayi, bwana, Abusa Branham, ine—ine sindinamvepo za inu.”

Ine ndinati, “Ine ndimapempherera odwala.” Iye analibe nazo chidwi zimenezo. Iye samafuna kuti mnyamata wake afe, ali wochimwa.

¹⁶³ Ine ndinadzalowa mmenemo; iwo anali ndi geti yakale pamenepo yokhala ndi chokokera chikulendewera pa iyo choikokera mmbuyo (mwinamwake ambiri a inu Akummwera simungadziwe chimene icho chiri), koma, kuti getiyo idzikhala yotsekedwa. Ndipo ine ndinayenda kulowa mnyumbamo, mu yaying’ono, kwambiri, yachikale, ya zipinda ziwiri (imawoneka ngati pang’ono...zomwe timadzitcha pang’ono “nyumba ya mfuti”) monga, itakhala pamenepo; pamakhala chipinda *apa*, ndipo ndicho chipinda chochezera, chipinda chogona, ndi zonse pamodzi; ndi khitchini kumbuyo *uko*. Pamene ine ndinadzalowa...Anali malo aang’ono opentedwa laimu, ndi abwino, otseguka mbali, ndi matabwa olukana. Chotero ndiye...Ayi, ndikukhulupirira kuti anali ndi pepala la phula pamwamba pa denga, Ine ndikukumbukira ndikuwona thovu lalikulu, ngati la mame, litapachikika pamwamba pake.

¹⁶⁴ Ndiye pamene ndinadzalowa, panali chikwangwani chikulendewera pamenepo pakhomo, chikuti, “Mulungu Adalitse Nyumba Yathu.” Pomwe apa pakona panali bedi lakale kuno, ndi lina cha apa. Apo panali munthu wamkulu kwambiri (panalibe chopondera pansa), mnyamata wamkulu kwambiri, mwana wamkulu wowoneka-bwino ataima pamenepo. Ine ndikuganiza iye anali...wolemera mapaundi handiredi ndi seventy kapena eyite, pafupifupi mapazi sikisi. Ndipo anali ndi bulangeti mdzanja lake, akuti, “Uhm. Uhm.”

¹⁶⁵ Ndipo iye anati, “Mwana wa amayi.”

166 Ndipo ine ndinaganiza, “Mwana wa amayi.” Ndipo komabe iye anali ndi—anali ndi matenda opatsirana, chindoko. Ndipo iye—iye amafa.

167 Ndipo iye anampsyompsyona iye pa mphumi, ndipo anamusisita iye monga choncho, anati, “Mwana wa amayi.”

168 Bwanji, mtima wanga unangokula. Ine ndinaganiza, “Inde, ngakhale utakhala wazama bwanji mu tchimo, iwe ukadali mwana wakebe.” Kenako ine ndinaganiza, “Onani, ziribe kanthu kuti anali woipa bwanji, iye akadali apobe ‘Mwana wa amayi.’” Ndipo ine ndinaganiza, “Mulungu anati, ‘Mayi akhoza kuiwala mwana wake woyamwa; koma Ine sindingakhoze konse kukuiwalani inu, chifukwa dzina lanu linazokotedwa mzikatho za dzanja Langa.’” Mukuona? Izo zingatheke bwanji!

169 Ine ndinayang’ana pa woyera wokalamba wosauka uja akuyenda kuzungulira pamenepo. Iwe umakhoza kudziwa, m’bale, iye analibe chirichonse mnyumbamo; koma iye anali ndi chinachake mnyumbamo chimene nyumba iliyonse mu Indiana kapena kwina kulikonse iyenera kukhala nacho; ameneye ndi Mulungu. Ine ndingakonde nditakhala nazo izo kuposa kukhala ndi nyumba yayikulu yabwino yokhala ndi atsikana odzivula, ndi zonsezi zanyansi, zinthu zoyipa. Baibulo lakale litakhala pamenepo pamene Ilo linali litatsegulidwa, masamba akale atakwinyika mwa Ilo.

170 Ine ndinamuyang’ana iye. Ndipo iye anati, “Abusa abwera kudzakupempherera iwe, wokondedwa.”

171 Iye akuti, “Uhm. Uhm. Mdima. Uhm.”

172 Ndipo ine ndinati, “Iye akuti chiyani?”

Iye anati, “Iye sakudziwa. Dokotala akuti, ‘Iye wachita misala.’” Anati, “Iye akuganiza kuti ali kunyanja yayikulu kwinakwake, ndipo iye akuyendetsa ngalawa, ndipo iye watayika.” Ndipo anati, “Ndizo zomwe ine sindingathe kupirira nazo, Abusa: kudziwa kuti mwana wanga akufa, wotayika.” Ndipo iye anati, “ine ndikudziwa kuti inu mwabwera kudzandithandiza ine, chifukwa Ambuye anandiuza kale ine.”

Ine ndinati, “Ine ndimupempherera iye,” ndipo ine ndinati, “mwinamwake Ambuye amuchiritsa iye.”

173 Iye analibe nazo chidwi zimenezo, iye amangofuna kuti iye adzuke ndi kunena kuti iye ‘wapulumutsidwa.’ Ndizo zonse, bola ngati iye wapulumutsidwa. Ziribe kanthu, iye ayenera kupita mulimonse, koteru, nthawiina; bola ngati iye wapulumutsidwa! Oh, ngati ife titangokhala ndi kaganizidwe kameneko! Kwathu Kwamuyaya kuja, iye ankadziwa kuti iye adzakakhalanso ndi iye mtsogolo.

Anati, “Ngati nditangomumva iye akunena kuti ‘ndapulumutsidwa.’”

Ine ndinati, “Tiyeni tiwerame.” Ndipo iye anagwada pansi. Ndipo ine ndinangogwira mapazi ake, ndipo mapazi ake anali akuzizira kwenikweni ndiponso akunyeta. Ndipo ine ndimalephera kukokera chofunda pa iwo, pang’ono—bulangeti lopyapyala pang’ono limene anali atafunda pamenepo; ndipo anangovala kabudula wake, inu mukudziwa.

174 Ndipo chotero iye . . . Ndipo iye anali akukokera iye mmbuyo monga choncho, akungoganiza kuti iye anali mmenemo. Iye anagwira chimenecho, ndi kumaganiza kuti akupalasa nkhaifi. Iye anakhala akunenabe kuti, “Muli mdima kwambiri. Uhm. Uhm. Muli mdima kwambiri.” Chotero ndiye iye anayesera kuti ayankhule ndi iye; ndipo iye akungonenabe, “Muli mdima ndipo mukuzizira,” akukoka basi.

175 Ndiye ine—ine ndinamuyang’ana iye pang’ono, ndipo iye anagwada pansi pamenepo, ndipo ine ndinati, “Azakhali, kodi inu mungatitsogolere ife mu pemphero?”

Iye anati, “Inde, bwana.”

176 Iye yekha, ndi ine, ndi mnyamatayo, ndi Mzimu Woyera mchipindamo, ndizo zonse. Woyera wachikulire uja anapemphera. Mai! Pamene iye anayankhula ndi Iye, iwe umadziwa kuti iye anali atalankhulapo ndi Iye kale. Inde, bwana! Iye ankadziwa yemwe iye amalankhula naye. Iye anati, “Ambuye, ine sindikudziwa chomwe Inu mutachite,” iye anati, “koma zonse ziri monga momwe Inu munanenera izo.”

177 Oh, mai! Oh! Ndine wokondwa kwambiri, ndine wokondwa kwambiri kuti Iye akadali Yesu yemweyo anali kumbuyo uko ndi oyera amenewo kumbuyo uko. Iye akadali Yesu yemweyo lero.

178 Ndipo ine sindinamufunse konse za chipembedzo chake, kaya iye anali wa Baptisti, wa Chipentekoste, kapena chiyani. Imeneyo siinali ntchito yanga. Ine ndinali—Ine ndimangotsatira Mzimu Woyera, ndipo iye anali kuchita chinthu chomwecho. Ife tinkafuna kuti tiwone zomwe Iye ati achite.

179 Chotero ife tinagwada pansi, ndipo iye anayamba kupemphera. Pamene iye anatsiriza kupemphera, iye anadzuka nampsyopsyona mutu wake, anati, “Mulungu, dalitsani mwana wanga.”

180 Ndipo kenako iye anati, “Tsopano kodi inu mungapemphere, Abusa?”

181 Ndipo ine ndinati, “Inde, amayi.” Ndipo apo pomwe inali pafupifupi hafu pasiti eyiti, mwinamwake kotara kuti ikwane naini, ndipo ine ndinali mkati . . . mamailosi awiri kuchokera pamalopo, ndipo—ndipo ndege imanyamuka seveni koloko; ndipo ine sindimadziwa kuti ndituluka liti.

182 Chotero ine ndinayika manja anga pamapazi ake, ine ndinati, “Atate Akumwamba, ine sindikumvetsa izi. Ndipo Inu . . . ine—ine ndimayenera kuti ndikwere ndege

kanthawi kapitako, pafupifupi ora ndi theka lapitalo. Inu mumangopitirira kumati, 'Kaziyenda,' ndipo ichi ndi chinthu chokhacho chimene ine ndapezekera panobe. Ndipo iye ananena kuti Inu . . . iye anandiwona ine ndikubwera. Ngati zimenezo—ngati zimenezo munali Inu, Ambuye, ndiye ine sindikudziwa choti ndichite koma kungoika manja anga pa mnyamatayu.”

¹⁸³ Iye anati, “Oh, mama,” anati, “mukuwala muno tsopano.” Ndipo pafupifupi maminiti faivi kuchokera pamenepo, iye anali atakhala pambali pa bedi, ndi manja ake atawakumbatira amayi ake.

¹⁸⁴ Ine ndinatuluka, ndinathamangira kumeneko ndipo ndinakakwera galimoto, ndipo ndinathamangira ku hotelo kukatenga sutikesi yanga. Ndipo ndimaganiza kuti ndipita ndi kukadikirira, mwinamwake kudikirira tsiku limodzi kapena awiri mmasiku amenewo. Inu mukudziwa momwe izo zimakhallira zovuta nkondo itangotha kumene kuti upeze ndege, chotero ine ndinaganiza, “Ine ndiyenera kudikirira masiku angapo.”

¹⁸⁵ Ndipo ine ndinakwera mgalimoto ndipo ndinathamangira uko, bwalo la ndege. Basi pamene ine ndinafika kumeneko, iwo anati, “Ndege nambala 196 yaku Louisville, Kentucky, tsopano ikunyamuka.” Mulungu anandigwirira ine ndege imeneyo pansi, monga choncho. Oh, ine ndikukhulupirira zimenezo!

¹⁸⁶ Pafupifupi zaka ziwiri kuchokera pamenepo, ine ndimapita kumusi pa sitima, ndikupita uko ku Arizona, kwa M'bale Sharrit, kumeneko ku msonkhano. Ndipo chotero ine ndinali woti nditengana ndi M'bale Moore ndi iwo. Ndipo chotero pamene ine ndinapita kumeneko, ine ndinaima pamenepo ku Memphis. Ndipo sitimayo inalowa mkati, ngati inu nonse mukudziwa momwe iyo imakhotera kupita kumadzulo monga chonchi, ndipo kenako imabwerera mmbuyo ndi kudzatembenuka mopotoloka ndi kuzimitsa.

¹⁸⁷ Ndipo masangweji awo pa sitima, iwo amafuna pafupifupi masenti sikisite pa chidutswa cha iwo. Ndipo ine ndikhoza kuzigula izo ndi masenti teni, fifitini, inu mukudziwa, uko kwina kwakenso. Ndipo ine ndinangodikirira mpaka sitima itaima, kuti ndidzipezere masangweji ena. Ine ndinali woti ndikukadzipezera ha- . . . thumba lodzaza ndi zitumbuwa, ndipo ndikukhaladi ndi chisangalalo chenicheni kumeneko. Chotero ine ndinalumphira panja ndi kuthamangira mmusi kudutsa kumeneko mofulumira kwenikweni, kuti ndikafike pogulitsira zitumbuwa; ndikuyang'ana yang'ana, iyo ikhala pamenepo pafupifupi maminiti sarte.

¹⁸⁸ Ndipo chotero ine—ine ndinayamba kupeza zitumbuwa zina, ndipo ndinamumva winawake akuti, “Moni, pamenepo, Abusa!” Ndipo ine ndinayang'ana pozungulira, chipewa chofiira

chaching'ono, atayima pamenepo akuphethira maso ake, inu mukudziwa, anati, "Simukundidziwa ine, sichoncho inu?"

"Sindikukhulupirira ine ndikutero, mwana."

Bwerani kuno, anati, "Ndiyang'aneni ine bwino!"

Ndipo ine ndinati, "Eya?" Ine ndinati, "Ine sindikukhulupirira kuti ine ndikukudziwa iwe."

Iye anati, "Ine ndikukudziwani inu!" Anati, "Ndinu Abusa Branham!"

Ndipo ine ndinati, "Eya, uko nkulondola." Ine ndinati, "Kodi iwe unayamba wakhalapo mu umodzi wa misonkhano yanga?"

Anati, "Ayi, bwana!" Anati, "Inu mukukumbukira mmawa uja inu munabwera ku nyumba ndipo amayi anga anali a- . . .?"

"Oh!" Ine ndinati, "Iwe si ameneyo!"

Anati, "Inde, ine ndi iyeyo! Inde, ine ndi iyeyo!" Iye anati, "Abusa," anati, "Ine ndinachiritsidwa, wamphamvu, ndipo wabwinobwino. Ndipo osati zokhazo, koma ndine Mkristu tsopano!"

¹⁸⁹ Ambuye alemekezeke! Oh!

Anasonkhana mchipinda chapamwamba,
Onse akupemphera mu Dzina Lake,
Anabatizidwa ndi Mzimu Woyera,
Ndipo mphamvu ya ntchito inabwera;
Tsopano chimene Iye anachita kwa iwo tsiku
limenero

Iye adzakuchitirani inu zomwezo, (Kodi sindinu okondwa?)

Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine
mmodzi wawo.

Mmodzi wawo, mmodzi wawo,
Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine
mmodzi wawo, Aleluya!

Mmodzi wawo, ndine mmodzi wawo,
Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine
mmodzi wawo.

Iwo alibe maphunziro akulu ndi zinthu:

Chotero anthu awa akhoza kusakhala
ophunzira,

Kapena kubwekerera za kutchuka kwa
mdziko,

Onse analandira Pentekoste wawo,

Anabatizidwa mu Dzina la Yesu;

Ndipo akunena tsopano, mtali ndi mfupi,

Mphamvu Yake ndi yomweyobe,

Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine
mmodzi wawo.

Mmodzi wawo, ndine mmodzi wawo,
 Ndine wokondwa kuti ndinganene kuti ndine
 mmodzi wawo, Aleluya!
 Mmodzi wawo, mmodzi wawo,
 Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine
 mmodzi wawo.

Bwera, m'bale wanga, udzafune mdalitso uwu
 Womwe udzatsuke mtima wako ku tchimo,
 Udzayambitsa mabelo achimwenwe kulira
 Ndipo udzayika moyo wako pamoto;
 Oh, ukuyaka tsopano mkati mwa mtima
 wanga,
 Oh, ulemelero ku Dzina Lake,
 Ndine wokondwa kuti ine . . .

Tsopano gwiranani chanza ndi winawake kutsogolo,
 kumbuyo, ndi mozungulira:

Oh, mmodzi wawo, mmodzi wawo,
 Ndine wokondwa kuti ndingati ndine mmodzi
 wawo, Aleluya!
 Mmodzi wawo, mmodzi wawo,
 Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine
 mmodzi wawo.

Mmodzi wawo, mmodzi wawo,
 Ndine wokondwa kwambiri . . . ? . . .
 . . . mmodzi wawo,
 Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine
 mmodzi wawo.

Ndine mmodzi wawo, mmodzi wawo,
 Ndine wokondwa kuti ndingati ndine m'modzi
 wawo, Aleluya!
 Mmodzi wawo, mmodzi wawo,
 Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine
 mmodzi wawo.

¹⁹⁰ Chipembedzo chakale ichi ndi chiti? Icho chinayambira
 kumbuyo *kuno*, ndipo icho chikudontha njira yonse mpaka
 mmusi ndi Magazi a Yesu Khristu. Oh, mai! Oh, ndine wokondwa
 bwanji chifukwa cha Uthenga! Oh! Oh, inde, bwana!

Ukuwukha magazi, inde, ukuwukha magazi,
 Uthenga wa Mzimu Woyera uwu ukuwukha
 magazi,
 Magazi a ophunzira (ofera, onse mmusi),
 amene anafera Choonadi,
 Uthenga wa Mzimu Woyera uwu ukuwukha
 magazi.

Tsopano, kodi Iwo ndi Uthenga wa mtundu wanji? Monga
 Iwo unayambira pa Pentekoste, mwaona.

Woyamba kufera dongosolo la Mzimu Woyera
 ili,
 Anali Yohane Mbatizi (Mwaona, iye
 analandira, mmimba mwa amayi ake, inu
 mukudziwa.) . . . anafa ngati munthu;
 Kenako anabwera Ambuye Yesu, iwo
 anamupachika Iye,
 Iye analalikira kuti Mzimu udzapulumutsa
 anthu ku tchimo.
 Unapitirirabe kuwukha magazi, inde,
 ukuwukha magazi,
 Uthenga wa Mzimu Woyera uwu ukuwukha
 magazi,
 Magazi a ophunzira amene anafera Choonadi,
 Uthenga wa Mzimu Woyera uwu ukuwukha
 magazi.

Inu simungakhoze kuwupanga Iwo bungwe! Huh-uh!

Kunali Petro ndi Paulo, ndi Yohane
 waumulungu,
 Anapereka miyoyo yawo kuti Uthenga uwu
 uwale;
 Anasakaniza magazi awo, ndi aneneri akale,
 Kutu Mawu owona a Mulungu akhoze
 kunenedwa moon.

Umawukhabe magazi, inde, ukuwukha
 magazi,
 Uthenga wa Mzimu Woyera uwu ukuwukha
 magazi,
 Magazi a ophunzira amene anafera Choonadi,
 Uthenga wa Mzimu Woyera uwu unali
 kuwukhabe magazi.

Kuli miyoyo pansu pa guwa, ikulira, “Mpaka
 liti?”
 Kuti Ambuye alange amene anachita zolakwa;
 Koma akhalapo ena ati adzapereke magazi a
 moyo
 Chifukwa cha Uthenga wa Mzimu Woyera uwu
 ndi kusefukira kofiira.

Ukuwukhabe magazi, inde, ukuwukha magazi,
 Uthenga wa Mzimu Woyera uwu ukuwukha
 magazi,
 Magazi a ophunzira amene anafera Choonadi,
 Uthenga wa Mzimu Woyera uwu ukuwukha
 magazi.

¹⁹¹ Tsopano, kuyambira nthawi ya Pentekoste, ndi ofera a Pentekoste, mpaka mu mpingo wa Efeso, mpaka ku Pergamo, mpaka ku Tiyatira, kupitirira mpaka—ku Sarde, mu wa Efeso . . .

kapena wa Filadelfia, ndipo mpaka mmusi ku Laodikaya. Ndipo tsopano kunachitika chiyani. . .kumusi kuno? Monga Baibulo linanena, chirichonse chimabwera mmenemo, ndipo chirombo ichi chidzawuka mu United States.

¹⁹² Inu mukukumbukira masomphenya omwe anawerengedwa pano, 1933? Ine ndimapita. . .Tchalitchi chinali chisanamangidwe nkomwe. Sindinkadziwa kuti masomphenya ndi chiyani, ndinazitcha izo “chizimbwizimbwi.” Ine ndinali chabe mlaliki wachichepere wa Baptist, ndipo ife tinali. . .

¹⁹³ Moyo wanga wonse ine ndimawona masomphenya amenewo, ndipo ndimupempha aliyense kuti adzuke ndi kunena ngati amodzi a iwo analepherapo konse. Ayi, sizinateropo! Izo sizingatheke! Mukuona? Izo sizingatero!

¹⁹⁴ Ndipo tsopano, ndipo pamene ine ndimayamba Sande sukulu ine ndinalowa mu chizimbwizimbwi. Ife tinali nazo kuno kunyumba yakale ya Masonic, malo a Charlie Kern, gulu laling'ono la ife. Ndipo ine ndinamuwona Purezidenti Roosevelt uyu akutsogolera dziko ku nkondo ya padziko lonse. Ndinaneneratu! Ine ndinati, “Ndipo pali ma ism atatu: Nazi, ndi Fascism, ndi Communism.” Ine ndinati. . .(Ndi angati muno akukumbukira?) Ine ndinati, “Ikani maso anu pa Chikominisi, izo zonse zidzasunthira mmenemo.” Ine ndinati, “Ethiopia, Mussolini adzapita ku Ethiopia, koma iye adzakalepherako.” Ndipo ine ndinati, “Ife potsiriza tidzapita ku nkondo ndi Germany, koma” Ine ndinati “Germany adzalimbikitsidwa, mumulu waukulu kwambiri wa konkire.” Zaka leveni Maginot Line asanamangidwe, zaka leveni.

¹⁹⁵ Ine ndinati, “Kenako nkondo ikadzatha. . .Ife tidzapambana pamapeto pake. Ndipo nkondo ikadzatha, izo zidzachitika kuti sayansi idzapanga zinthu zazikulu.” Ndipo ine ndinati, “Pamene iwo adzatero, iwo apanga galimoto, ndipo magalimoto mopitirira adzasintha mawonekedwe.” (Inu mukudziwa momwe iwo ankawonekera mu '33.) Tsopano ndiye, anati, “Iwo adzakhala ngati mazira, azidzawoneka ngati mazira. Pakuti ine ndinawona pa msewu waukulu, msewu waukulu wopambana, galimoto ikuyenda mu msewu imene inalibe chiwongolero chirichonse mmenemo. Iyo imawongoleredwa ndi mphamvu.” Iwo ali nayo iyo pakali pano.

¹⁹⁶ Ine ndinati, “Nthawi imeneyo. . .Tsopano iwo akuloleza akazi kuvota; ndipo akazi, pakuvota, potsiriza pake. . .” Ine ndinati, “Fuko lino ndi fuko la mkazi, ilo limadziwika ndi mkazi. Ndi mkazi mpaka kudutsa mu uneneri, paliponse; ndi nambala sartini paliponse mu uneneri.” Ndipo ine ndinati, “Ndi dziko la mkazi, iye ali ndi ufulu wake kuno. Ndipo iye adzawuwononga iwo, iye ndi amene amaliwononga dziko lapansi.”

¹⁹⁷ (Ndipo, Roy, ine ndalandira makalata ako pa zimenezo, mkazi wamkulu ameneyo. . .“Mlandu uliwonse. . .Tingakhale

nawo...Ine Ndikanazijambula izo tsopano mpaka: mulandu uliwonse womwe unachitikapo mu United States uyu, mkazi anali kumbuyo kwake.” Ndiko kulondola ndendende. Amenewo ndi akazi amakhalidwe oyipa, inu mwaona, ndi zinthu.)

¹⁹⁸ Tsopano, chotero ndiye ine ndinati, “Kudzakhala mu nthawi imeneyo, panthawi imeneyo akazi azidzalolezedwa kuvota, ndipo iwo adzasankha munthu wolakwika.” Iwo anachita izo pachisankho chomaliza ichi. Uko nkulondola. “Zomwe ziti zidzayambitse linga. Nthawi imeneyo zidzachitika kuti—kuti kudzakhala mkazi wamkulu adzauka mu United States, iye adzavala mokongola,” ndipo ine ndinaziika mokutira: “(mwinamwake mpingo wa Katolika).” Mukuona? “Yemwe ati adzatenge ulamuliro pa mphamvu, adzawapambana enawo mu United States. Iye adzakhala wokongola ukamamuyang’ana, koma iye adzakhala wamtima wankhanza momwe iye angathere.”

¹⁹⁹ Ine ndinati, “Kenako ine ndinayang’ananso, ndipo ine ndinawona United States atangophulika mzidutswa. Panalibe kanthu kamene kanatsalira pa iye.”

²⁰⁰ Ndipo ine ndinaneneratu pamenepo. “Tsopano ichi, icho chinali PAKUTI ATERO AMBUYE.”

²⁰¹ Ndipo talingalirani! Mwa maulosi faivi mwa seveni aja, achitika kale.

²⁰² Mpingo kuti ugwire, mpingo wa Katolika. Ndi kudza kwa nthawi yotsiriza.

²⁰³ Ndipo ine ndinati, “Ine ndinawona, zinkawoneka ngati panali zitsa zikuyaka; miyala, inaphulitsidwa; ndipo United States yense amangowoneka wopanda kanthu, atangokhala monga choncho, momwe ine ndimakhoza kuwona pamene ine ndinali nditaima.”

²⁰⁴ Ndipo ine ndinati, “Ine ndikuneneratu, malingana ndi momwe nthawi ikuyendera, zidzakhala nthawi ina pakati pa chaka chino ’33 ndi ’77.” Ndipo izo zidzayenera kudzafinya mwamphamvu kowopsya kuti zidutse pamenepo.

²⁰⁵ Ndipo ife tikukhala pa botolo la onga, abwenzi. Chirichonse chakonzeka.

²⁰⁶ Oh, koma Atate athu Akumwamba wofunika Yemwe analonjeza, Yemwe analonjeza! Kodi sizodabwitsa kukhala wantchito wa Khristu? Zinthu zonse zimene Iye analonjeza! Ndipo taganizani; ife tiri nawo mwayi. Iye akukhala moyo pomwe pano. Iye ali ndi ife kumene tsopano, akudziwa chinsinsi chirichonse cha mtima uliwonse, amadziwa zonse za inu; moto woyaka umenewo ukuyenda kudutsa mmitima yathu, akudziwa zonse za ife, amatikonda ife.

²⁰⁷ Ndipo kodi sindinu okondwa kukhala mgulu laling’ono lochepa limenelo, usikuuno, lomwe limasunga Chikhulupiriro?

Pakuti linali lamulo Lake, “Musawope, kagulu kankhosa, ndi chifuniro chabwino cha Atate Wanu kuti akupatseni inu Ufumu. Ndipo ntchitoyi ikanapanda kufupikitsidwa, sipakanakhala mnofu uliwonse ukanapulumsidwa.” Mwaona, ife tiri kumene pa nthawi yotsiriza.

²⁰⁸ Achipentekoste akukhala ozizira, ofunda, olavulidwa mkamwa mwa Mulungu.

²⁰⁹ Gulu laling'ono kwambiri lomwe latulutsidwa apa, apang'ono okha, koma mmenemo mudzabwera: “Taonani, Mkwati akubwera!” Ndipo pamene izo zidzatero, uliwonse wa maulonda awa, ulonda uliwonse wa maulonda awa, kuti . . . Kumbukirani, pali maulonda seveni a iwo. Ndipo ife tiri mu ulonda wotsiriza kumene *wuu*. Koma aliyense wa anamwali amenewo mmbuyo kudutsa *apa* anawuka. Ameni! Oh, chinali chiyani icho? Mzimu Woyera womwewo.

²¹⁰ Ndiye pamene mpingo udzakhala utapita mu . . . Monga ife tinatengera Lamlungu usiku, Yosefe kuti akazidziwitse yekha kwa Israeli, abale ake, iye anamubalalitsa mkwatibwi wake, chirichonse, ndipo anawabweza iwo kupita kunyumba ya chifumu. Ndipo iye anayima yekha ndi Ayuda, ndipo anati, “Ndine Yosefe, m'bale wanu.”

²¹¹ Muziike izo pomwepo mu Lemba pamene iwo anati iwo adzakhazikitsa tsiku lachisoni, ndi nyumba iliyonse ikudzilirira yokha.

²¹² Iwo anati, “Kodi Inu munazitenga kuti zipsyera zimenezi?”

Anati, “Mmanja mwa . . .”

“Mmanja Mwanu?”

Anati, “Mnyumba ya abwenzi Anga.”

²¹³ “Iwo amene anamupyozza Iye adzayang'ana pa Iye.” Ndipo pamenepo Iye adzayima, Yosefe.

²¹⁴ Iye anati, “Musatero . . .” Monga Yosefe anati, “Musadzikiwiyire nokha, chifukwa Mulungu anachita izo kuti apulumutse moyo.” Chiyani? Moyo wa Mpingo, Amitundu, “Chifukwa cha Dzina Lake, anthu ochokera mwa Amitundu.”

²¹⁵ Oh, ife tiri kumapeto, abale anga. Ife tiri pano! Lodala likhale Dzina la Ambuye! Tiyeni tiyimbe nyimbo yabwino yakale iyi, monga abale ndi alongo achipentekoste, limodzi. Tsopano, inu mukuti, “Chabwino, ndine wa Baptisti.” Koma ngati inu muli nawo Madalitso Achipentekoste, ndinu wachipentekoste. Uh-hum. Chabwino. Chabwino:

Chodala chikhale chimango chimatimangiriza
Mitima yathu mu chikondi Chachikhristu;
Chijanano cha malingaliro apaubale
Chiri chonga chiya chakumwamba.

216 Tsopano mvetserani, abwenzi. Ngati pali aliyense pano pakati pathu, kuti ngati paliponse paulendo wa moyo, kuti kuwawidwa pang'ono kuja kwabwera mu mtima mwanu, (Ndimvereni ine!) zichotseni izo pamenepo tsopano. Pezani izo, musalole china chirichonse. . .

[Mlongo akuyankhula mu lirime lina. Malo opanda kanthu pa tepi. M'bale akutanthauzira—Mkonzi]. Ameni. [M'bale akuyankhula mu lirime lina ndipo kenako akutanthauzira]. Ameni. Ameni.

217 Ambuye Yesu, ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha mauthenga awa. Izo zimatikondoweza ife, Ambuye podziwa kuti ife sitinaleke koma tasunga chikhulupiriro. Oh, ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Mzimu upitirize kukhala mu mpingo. Tisungeni ife pafupi kwa wina ndi mzake, Atate. Tisungeni ife ndi Inu. Ndipo muyende pakati pathu, Ambuye, mu m'badwo wotsiriza wa choyikapo nyali uwu womwe ife tikukhalamo. Mukhale Kuwala kwathu. Muwalire pa ife, nthawi zopambana izi za mdima, Ambuye, pakuti ife tikuzindikira kuti *choyikapo nyali* ndi *nyenyezi* zikuyankhula za “mdima.” Ndipo Ambuye, ndife okondwa kuti ndife ana a Kuwala, tikuyenda mu Kuwala kwa Mulungu. Sindife omangiririka padziko ndi zinthu zapadziko lapansi izi, koma ndife ana Anu. Momwe ife tikukuthokozerani Inu chifukwa cha zinthu izi.

218 Ife tikukuthokozani Inu potumiza mauthenga awa monga chitsimikiziro cha Mawu Anu. Mulole Inu mukhale nthawizonse wolemekezeka pakati pathu, Atate. Inu mutitetezere ife ku zowawa zonse za dziko lapansi. Tisungeni ife oyeretsedwa, kuti miyoyo yathu ikhale yangwiro ndi yoyera ndi yopatulika pamaso Panu. Mulole Magazi a Yesu Khristu achitire izi aliyense wa ife, Ambuye. Chotsani pakati pathu, ngati pangakhale chirichonse chomwe sichiri bwino. Chichotseni icho kwa ife, Ambuye. Ili ndi ora la nthawi zofufuza.

219 Misonkhano iyi imapangidwira cholinga chimenecho kuti ifufuze mitima yathu. Inu munati malawi amoto amenewo a maso Anu, “amafufuza ndipo amadziwa minyewa ya mtima.” Inu ndithudi mmatero, Atate. Ndipo muyankhulenso mobwezera kwa ife ndipo kenako nkutiuza ife kuti tipange. . . tidzisunge tokha okonzeka kuti ora likuyandikira.


220 Oh, momwe ife tikukuthokozerani Inu chifukwa cha izi, Atate. Ife tidzachita zimenezo ndi zonse zomwe ziri mwa ife mwa chisomo Chanu. Ameni.

221 Oh, kodi inu simukumukonda Iye? Tsopano, ngati pangakhale mlendo pakati pathu, umo ndi momwe izo zinaliri pachiyambi. Pamene Yesu anali kuno padziko lapansi, Iye anati, winawake anamufunsa Iye za nkhani ya chikwati ndi chilekano kapena chinachake, Iye anati, “Izo sizinali chomwecho kuyambira pachiyambi.” Tiyenera kubwerera ku chiyambi.

²²² Ndiye ngati chiyambi chinali mpingo wa Pentekoste ndipo Iye ndiye Mpesa, ife ndife nthambi, nthawi iliyonse pamene Mpesa ubala mpingo, udzakhala mpingo wa Chipentekoste, nthambi ya Chipentekoste; chinthu chomwe chomwecho chinali pachiyambi, (Mukuona?), nthawi iliyonse. Tsopano, inu mukhoza kumezanitsa mipesa ina mmenemo ndipo iyo idzabereka chipatso chake. Inu mukhoza kutenga mte—mtengo wa lalanje ndi kuyikapo mandimu pa iwo, iwo udzabala mandimu wokhala moyo kuchokera pa malalanje. Mukaika mphesa pambali pake, ndipo iwo udzabala mphesa chifukwa ndi chipatso cha zowawasa.

²²³ Chotero mabungwe awa, zipembedzo ndi zinthu, zakakamira kumeneko, kumaitana Akhristu, iwo akhoza kukhala moyo ndi moyo Wachikhristu. Ndiko kulondola ndendende, koma iwo adzabala zipatso zachipembedzo. Uko nkulondola. Chifukwa iwo angozikidwapo monga choncho. Koma ngati nthambi imeneyo payokha idzaphukire a... kapena ngati Mpesa umenewo udzaphukire konse nthambi, iyo idzakhala... iyo idzalemba Bukhu la Machitidwe kumbuyo kwake. Ndiko kulondola ndendende. Chifukwa ndi chimene chinachitika nthawi yoyamba. Nthambi iliyonse yomwe idziphukitsa yokha idzakhala ndi malalanje, iliyonseyo. Ndipo Baibulo layankhula izo; iwo unali ndi nthambi thwelofu pa iwo.

²²⁴ Oh, ndine wokondwa kwambiri kukhala moyo pansu pa nthambi imeneyo, sichoncho inu? Inde, bwana. Oh, ndi zodabwitsa.

²²⁵ Chabwino, kumbukirani mawa usiku tsopano pa m'badwo wa Fila...wa Sarde. A...?...kubwera kwa bungwe la Chilutera, Martin Luther...?...


M'BADWO WA MPINGO WA TIYATIRA CHA60-1208
(The Thyatirean Church Age)

MAULALIKI A VUMBULUTSO LA YESU KHRISTU

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lachinayi madzulo, Disembala 8, 1960, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2022 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org